


# *DZIKO KAMODZINSO*

## *LIKUGAWANIKA PAKATI*

 Ameni. Ambuye akudalitseni inu. Inu mukhoza kukhala pansi. Zinamveka zabwino kwambiri kuti ndibwere muno usikuuno ndi kudzakumvani inu mukuwatamanda Ambuye, ndi kubwereranso kwathu ndi kudzamuwona aliyense. Ine ndakhala ndikuyembekezera ichi kuyambira Kuperekamathokoza kwapita pamene ine ndinali kuno, kuti ndidzabwerere ku kachisi wanga kachiwiri. [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ine sindikudziwa kumene iye anapita. Ndi uyu ali apayu. Ine ndikungodabwa ngati iye akanati anenebe “ameni” kwa izo, inu mukudziwa. [M’bale Moore akuti, “Ameni.”] Izo nthawizonse chimakhala chabwino kukhala pano. Ndipo ine ndimayembekezera, monga ine ndanenera, kuyambira pa Kuperekamathokoza kwapitaku.

<sup>2</sup> Ife tangochoka kumene ku New York City, kumene tinali ndi msonkhano wopambana. Ambuye anataliditsa ife kumeneko mwanjira yamphamvu. Ndipo ife tinali ku Morris Auditorium, ndipo gulu linadzaza mkati, ndipo chokwera ndi chotsika mmisewu. Ndipo iwo amakhoza kuyima kunjira uko, akuyembekezera. Ngati—ngati wina atalowa mkati, basi nkudzangoimirira, inu mukudziwa, ndipo angaganize, chabwino, chinachake; anthu ena, inu mukudziwa, amapita ku tchalitchi, ndipo kenako chinthu choyamba, chinachake chikanenedwa, chimene iwo samachikonda, amadzuka ndi kumachokapo. Ndipo iwo anali kunjira uko akuvota, ndani yemwe ati atenge mpando umenewo pamene iwo atuluka. Ndipo ine ndimabwera usiku uliwonse, ndipo pafupifupi kutalika kwa mdadada wa mzinda, ndipo iwo amakhala atawunjikana chokwera ndi chotsika mmisewu. Ndipo Ambuye anataliditsa ife ndipo anatipatsa ife miyoyo, ndipo machiritso ambiri aakulu anachitika.

<sup>3</sup> Ndipo kenako pa kadzutsa wa Amuna Amalonda, ife tinali ndi nthawi yopambana, anagulitsa matikiti awo. Ndipo—ndiyeno ine ndikuganiza iwo amayenera kuwalola mahandirede kuti alowe, amene analibe matikiti. Ndiye iwo anadzadzitsa mu tinjira, ndi pozungulira holo ndi zitseko, ndi zina zotero. Ndipo ife tinangokhala ndi nthawi yopambana kwambiri. Wansembe wa Episcopal ndi chirichonse kumeneko, ndipo Ambuye anataliditsa ife mochuluka.

<sup>4</sup> Ndipo kenako ife tinayima kwathu, kwathu kwina, mu Jeffersonville. Zooni, ine ndikukhala tsopano mu Tucson,

Arizona, monga inu mukudziwira, kwa zaka ziwiri zapitazi.

<sup>5</sup> Ndipo tsopano ine ndiri pa njira yobwerera ku Tucson tsopano, ku kadzutsa wa Amuna Amalonda sabata yamawa ku Phoenix. Kumene, pambuyo pa koyambirira kwa chaka, ife tikayamba msonkhano kumeneko, masiku pang'ono isanafike Business Men's International, ine ndikukhulupirira, kapena msonkhano wadziko lonse ku—ku Ramada Inn.

<sup>6</sup> Ndipo ndi chabwino kwambiri kukhala pano mu—mu mzinda wabwino uno wa Shreveport, usikuuno.

<sup>7</sup> Tsopano, kawirikawiri ine ndimayankhula nthawi yayitali. Koma ine ndiyetsesa mwakuthekera kwanga kuziyika izo pansi, maora atatu kapena anayi, mulimonse, kwa iyi ndi ku nthawi iyi. Ndipo ine ndikudziwa ine ndimangokutopetsani inu, koma, onani, ine sindimakuwonani inu pafupipafupi. Ndipo ambiri akumapita Kwawo ine ndisana . . . apita Kwawo ku Ulemelero ine ndisanakuwoneni inu kenanso, ndipo ine ndikuganiza, “Chabwino, uku kukhala kucheza kwathu komaliza padziko lapansi inu musananyamuke.” Ndipo kwambiri apita, sindikukayika, kuyambira nthawi ino chaka chathachi. Ndipo mwinamwake, ngati Ambuye achedwa, ndipo nkudzabwereranso chaka chamawa kapena nthawiina, iwo adzakhala ena owonjezera, pano usikuuno, mwinamwake inemwini. Ife sitikudziwa nthawi yomwe titi tidzaitanidwe. Ndipo, inu mukudziwa, Ambuye Yesu akhoza kubwera ngakhale misonkhano iyi isanathe usikuuno.

<sup>8</sup> Tsopano, monga inu mukundidziwira ine, sindine namatetule, sindine woyankhula. Ine—ine ndimangowakonda Ambuye ndi kuchita zomwe ine ndingathe kwa ulemelero Wake. Ndipo pamene ine ndayima pano pa nsanja iyi, ndikudziwa kuti munthu ameneyo monga M'bale Moore ndi amuna ambiri aakulu ayimapo pa nsanja ino, izo zimandipangitsa ine kumverera ngati—monga ngati . . . osati ndikusungulumwa, ine sindikutanthauza zimenezo. Koma, ine ndikutanthauza, galamala yanga ndi zinthu, ine ndimamverera ngati, ngati anthu akanati sanandikonde ine bwino kwenikweni, iwo bwenzi akudzuka ndi kumatuluka pamene ndikubwera pa guwa. Chotero iwo amangopirira nane ine, ndipo ndine wothokoza chifukwa cha izo. Tsopano . . .

<sup>9</sup> Koma nthawizonse ndimabwera ndi ichi—ndi cholinga ichi. Ine sindimabwera kuno kuti ndidzangowonedwa; ngati ine ndikanamatero, ine bwenzi ndikupita ku nyumba kwanu kukacheza, mwaona. Ine ndimabwera kuno kuti ndidzachite zopambana zomwe ine ndingathe kwa Ambuye Yesu Khristu, pamene ine ndiri kuno. Ine ndimabwera kuno osati kwa cholinga china koma kuti ndidzamutumikire Iye, ndipo mopambana momwe ine ndikudziwira, ndi kubweretsa kwa inu Mawu monga momwe Iwo aperekedwera kwa ine, kupempherera odwala anu

ndi osautsika. Tsopano, ife tikhala ndi usiku, kapena uwiri, M'bale Moore ndi ine tikhala pamodzi, kuti ife tipempherere odwala.

<sup>10</sup> Ndiyeno, usiku uliwonse, ife tikufuna munthu aliyense amene si Mkhristu, ndikuyembekeza chinachake chinenedwa kapena kuchitidwa, kuti inu mukhale Mkhristu. Ndipo ngati inu simuli, ngati inu mwakhulupirira kale pa Ambuye Yesu Khristu, ndi kumulandira Iye ndipo munabatizidwa, ndipo inu simunalandire Mzimu Woyera panobe, musalole kuti izi zidutse. Mungolola uwu ukhale usiku wanu. Chifukwa, kumbukirani, padzakhala maina ochuluka kwambiri pa Bukhu limenero. Ndipo pamene dzina lomaliza lidzawonjezedwa, ndizo zonse za izo. Ndipo lanu likhoza kumalizitsa Ilo.

<sup>11</sup> Pamene Mwanawankhosa anabwera ndi kudzatenga Bukhu kuchokera mdzanja lamanja la Iye amene anakhala pa Mpandowachifumu, limenero linali Bukhu la Chiwombolo. Ndipo maina amenewo anayikidwa mmenemo maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Pamene dzina lomaliza limenero linaitanidwa, Bukhu, dongosolo, china chirichonse chinawululidwa pamenepo, Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiwi zinatsegulidwa ndi Mwanawankhosa. Zinsinsi za Baibulo lonse zinabisidwa mmenemo. Ngati ife tikanakhala ndi nthawi, ine ndikanakonda kutero. . .

<sup>12</sup> Tangomaliza kumene Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiwi zimenezo, basi posachedwapa. Ine ndikufuna kuti ndidzadutse mu izo kenanso. Ndipo basi momwe Ambuye anataliditsira ife! Ambiri a inu mwamvapo za izo, ndipo munawerenga mu *Life* magazini, ndi zinthu, zinthu zimene zinachitika nthawi imeneyo. Pamene, iwo anajambula chithunzicho, ngakhale, cha Angelo seveni, monga zinanenedweratu pamene ife tinkapita Kumadzulo. Ndipo Iye anandiuza ine, miyezi itatu mmbuyo, kumene izo zikanadzakhala ndi momwe ine ndikanati ndidzayimire kumeneko, ndipo apo izo zinali! Ndipo a—ndipo makamera, oh, kwa mahandirede a mamailosi, anajambula chithunzi cha Iwo pomwe apo, ndendende basi. Zinanenedweratu ndendende! Ndipo ngati ine ndinayamba ndalalikirapo chirichonse chimene chinali chodzozedwa, mmoyo wanga, ndi *Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiwi*. Ndipo chotero ine ndikudzwiwa ife tiri ku nthawi ya kumapeto.

<sup>13</sup> Ndipo dzina lotsiriza likupita pa Bukhu limenero, kapena, dzina lotsiriza limene linawomboledwa, limene linaikidwa pa Bukhu limenero, izo zidzakhazikitsa izo, Iye akubwera kudzatenga chimene Iye anachiwombola. Ndipo iyo ikhoza kukhala nthawi yachilendo. Kodi inu munayamba mwaziganizirapo: anthu azidzapitirirabe kumalalikira, mpingo uzidzapitirirabe ngakhale kumaganiza kuti iwo akupulumutsa anthu. Zidzakhala nthawi itatha kwambiri pamenepo, izo zonse zitatha, mwaona, ndipo Uthenga udzapita kwa otayika

kwathunthu; chimodzimodzi monga momwe izo zinachitira m’masiku a Nowa, masiku seveni mu chombo. Izo zinatero mmasiku a Sodomu. Yesu Mwiniwake, Lake—gawo Lake lachitatu la utumiki Wake, Iye anapita ndipo anakalalikira kwa miyoyo yomwe inali yotayika Kwamuyaya, imene inali mu ndende, imene sinalape, kulezamtima mmasiku a Nowa. Ndipo ife sitikudziwa nthawi yanji yomwe zinthu izi zingadzachitike.

<sup>14</sup> Ndipo tiyeni tikhale ochenjezedwa. Osangoyima pozungulira, tiyeni tichite chinachake pa izo. Ngati sitiri pachiyanjano ndi Mulungu, tiyeni tikhale pachiyanjano ndi Mulungu.

<sup>15</sup> Nthawi ina, ine ndikuganiza, m’mutu wa 11 wa Mateyu, ine ndikukhulupirira iwo uli, cha pafupifupi ndime ya 6, kapena chinachake, ine sindiri wotsimikiza za izo. Ndi mutu wa 11, ine ndikutsimikiza kwenikweni. Ophunzira a Yohane anatumidwa ndi Yohane, nthawi ina, kuti akamuwone Ambuye Yesu, kuti akamufunse Iye ngati Iye analidi Mmodziyo, kapena azifunafuna wina. Iye anati, “Pitani mukamuwonetse Yohane zinthu zimene zikuchitika. Mukamuze iye, ‘Wodala ndi iye amene sakhumudwa mwa Ine.’”

<sup>16</sup> Ndipo kenako pamene iwo anawoloka phirilo, ndipo Yesu mwinamwake ankawayang’ana iwo, Iye anati, “Kodi inu munatuluka kudzawona chiyani?” Ndipo iwo... Anati, “Kodi inu munapita kukawona mtundu wina wa munthu wovala zovala zofewa?” Iye anati, “Iwo ali mnyumba za mafumu. Ndi bango logwedezeka ndi mphepo?” Iye anati, “Kodi inu munapita kukawona mneneri?” Anati, “Ine ndinena kwa inu, ndipo woposa mneneri. Ngati inu mungalandire zimenezo, uyu ndi iye amene mneneriyo amamukamba, Malaki 3, ‘Ndipo Ine ndidzakutumizirani wa mthenga Wanga pamaso pa nkhope Yanga.’”

<sup>17</sup> Ophunzira anafunsa nthawi ina za funso ili. Iwo anati, “Chifukwa chiyani alembi amati, aphunzitsi a Lemba, kuti, ‘Eliya akuyenera kubwera koyamba izi zisanachitike, zinthu zonsezi zidzachitika?’” Tsopano kumbukirani, Iye anali akuyankhula kwa ophunzira, osati kwa Afarisi. Ophunzirawo, iwo anati, “Chifukwa chiyani alembi amanena kuti, ‘Eliya akuyenera kubwera poyamba?’”

<sup>18</sup> Iye anati, “Eliya anabwera kale, ndipo iwo anamuchitira iye zomwe iwo analemba, ndipo inu simunadziwe izo.”

<sup>19</sup> Bwanji ngati tsiku lina inu mutapeza, ife tafika nthawi ya chisautso kapena chinachake, inu mudzati, “Chabwino, ine ndimaganiza Mkwatulo unali woti ubwere poyamba?” Mukuona? Ndipo liwu likanadzayankha ndi kukuuzani inu, “Mkwatulo unachitika kale, ndipo inu simunadziwe izo.”

<sup>20</sup> “Monga izo zinali m’masiku a Nowa, m’menemo anthu eyiti anapulumutsidwa ndi madzi, chotero izo zidzakhala

pa Kudza kwa Mwana wa munthu.” Anthu azidzapitirirabe, akumangoganiza kuti akuchita chinthu cholondola, ndipo izo zonse zidzakhala zitatha. O Mulungu, tichitireni ife chifundo! Tiyeni, tiyeni tifufuze, pakali pano mmausiku angapo otsatirawa, tiwone pamene ife tiri.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu kachiwiri.

<sup>21</sup> Ambuye Yesu, ndi zinthu izi mmalingaliro, ndipo zitaperekedwa ku mpingo uno, zitaperekedwa kwa anthu awa; Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu mupulumutse moyo uliwonse mu Shreveport, nthawi ino, umene unalembedwa mu Bukhu limenero. Ngati alipo ena pano amene sanapulumsidwe, Atate, mulole ili likhale ora limene iwo ati apulumutsidwe. Ngati alipo aliyense mwa osonkhana awa, usikuuno, mulole uno ukhale usiku wawo.

<sup>22</sup> Mudalitseni M'bale Moore, Mlongo Moore, ndi banja lawo, ana awo, ana a ana awo. Mulungu, ife tikungokuthokozani Inu chifukwa cha iwo. Ndi M'bale Lyle, M'bale Brown ndi onse—abale kuno ku mpingo, M'bale Don, ndi gulu labwino la anthu awa, mamembala onse pano, anthu wamba, ife tikungokuthokozani Inu chifukwa cha iwo.

<sup>23</sup> Ndipo tikupemphera, Atate Akumwamba, kuti kusunkhana kwathu pamodzi pano pa Kuperekamathokozi uku... Iko kukhoza kukhala Kuperekamathokozi komaliza komwe tidzakumane konse limodzi padziko lapansi lino, chotero, Mulungu, tiloleni ife titengerepo mwayi ndi kusunga nthawi. Ndipo ife tikuzindikira kuti—nthawi ikutha, ndipo ife tikufuna chirichonse chimene ife tingakhoze kuchita, chimene chiri mu mphamvu yathu, kuti tigwire ntchito ya Ambuye Yesu Iye asanabwere. Mwanjira ina, ine ndikumverera ngati Iye akutidikirira ife kuti—kuti timalizitse ntchitoyo. Chotero, tithandizeni ife, Ambuye, usikuuno, ngati munthu payekha, aliyense wa ife, kuti ife tikhoze kukhala okhudzidwa kwambiri ndi ena, kuti tipite panja mmisewu, kapena kupita mmadera, ndi—ndi kukabweretsamo otayika, kuti iwo akapulumsidwe.

<sup>24</sup> Adalitseni Mawu Anu. Mawu Anu ndi Choonadi, Ambuye, Choonadi chonse. Chotero ife tikupemphera, kuti pamene ife tikuyesetsa kuti tinyeme Mkate wa Moyo uwu, Choonadi, kwa anthu, kuti Mzimu Woyera ubwere, chifukwa cha thupi losweka lija pa Kalvare pamene tchimo linkayenera kuti liswe ilo, ndipo adzazigawaniza Iyemwini pakati pathu kachiwiri, mu chiyanjano mozungulira Mawu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

<sup>25</sup> Tsopano, ngati mungathe, ine ndikufuna inu mutsegule ndi ine. Ambiri a inu mumakonda kukhala ngati mumasunga a—Malemba pamene mtumiki akuwerenga, kapena mvangeri. Ndipo ine ndikufuna kuti ndiwerenge ena, usikuuno, kuchokera ku Deuteronome, mutu wa 4, kuyambira ndi ndime ya 7 mpaka

ya 14. Ndi Bukhu la Ahebri, mutu wa 14, ndime ya 25 kudutsa mpaka ya 29, kuphatikiza. Deuteronomie 4.

*Pakuti fuko lalikulu limene liripo ndi liti, limene Mulungu ali nalo pafupi ndi iwo, pakuti AMBUYE Mulungu wathu ali mu zinthu zonse zimene ife timamuyitanira Iye?*

*Ndipo ndi fuko liti limene liri lalikulu chotere, limene liri ndi malamulo ndi maweruzo olungama monga lamulo lonseli, limene ndayika pamaso panu lero?*

*Mungosamala kwa inueni, ndipo musunge moyo wanu mwakhama, kuti mungayiwale zinthu zimene maso anu aziwona, ndi kuti izo zingachoke pamtima panu masiku onse a moyo wanu: koma muwaphunzitse ana anu, ndi ana a ana anu;*

*Makamaka tsiku limene inu munayima pamaso pa AMBUYE Mulungu wanu mu—mu Horebu, pamene AMBUYE anati kwa ine, Sonkhanitsani anthu pamodzi, ndipo Ine ndidzawapangitsa iwo kumva mawu anga, kuti iwo adzaphunzire kundiwopa ine masiku onse amene iwo adzakhale moyo padziko lapansi, ndi kuti iwo aphunzitse ana awo.*

*Ndipo inu munabwera pafupi ndi kudzayima pansu pa phiri; ndipo phirilo linayaka moto kufikira pakati pa kumwamba, ndi mdima, ndi mitambo, ndi kukhuthala, ndi mdima.*

*Ndipo AMBUYE anayankhula ndi inu kuchokera pakati pa moto: inu munamva liwu Lake la mawu, koma simunawone mafanizo; koma munangomva liwu.*

*Ndipo iye anafotokoza kwa inu chipangano chake, chimene iye anakulamulirani inu kuti muchite, ngakhale malamulo khumi; ndipo iye anawalemba iwo pa magome awiri amiyala.*

*Ndipo AMBUYE anandilamula ine nthawi imeneyo kuti ndikuphunzitseni inu malamulo ndi maweruzo, kuti inu mukhoze kuwachita iwo m'dziko limene inu mukupita kukalilandira ilo.*

<sup>26</sup> Ndipo tsopano mu Bukhu la Ahebri, mutu wa 14, kuyambira ndi ndime ya 25.

*Muwone kuti inu musamukane iye amene anayankhula. Pakuti ngati iwo sanathawe amene anamukana iye amene anayankhula padziko lapansi, mochuluka ifenso sitidzathawa, ngati ife titembenuka kuchoka kwa iye amene akuyankhula kuchokera kumwamba:*

*Amene liwu lake pamenepo linagwedeza dziko lapansi: koma tsopano iye walonjeza, kuti, Kamodzinsu*

*ine ndidza, sindidzagwedeza dziko lapansi lokha, komanso kumwamba.*

*Ndipo mawu awa, Komabe kamodzi . . . kutanthauza kuchotsa kwa . . . zinthu zimene ziri zogwedezeza, monga ngati zinthu zimene zimapangidwa, kuti zinthu zimenezo zimene sizingagwedezeke zikhalebe. Apo . . .*

*Mwa ichi ife talandira ufumu umene sungasunthidwe, tiyeni tikhale ndi chisomo, chimene ife tingatumikire nacho Mulungu movomerezeka ndi ulemu ndi mantha aumulungu.*

*Pakuti Mulungu wathu ndi moto wonyeketsa.*

<sup>27</sup> Tsopano ine ndiri ndi zolemba pang'ono apa, ndi Malemba ena olembedwa, amene ine ndikufuna kuti ndilozere kwa iwo kwa maminiti pang'ono, monga ine ndingawutchule mutu uwu mutu wawung'ono wachirendo. Ndipo matepi awa ali okonzeka nthawi iliyonse yomwe aliyense angawafune iwo. Bambo Maguire apa adzakhala wothekera ku—kukupatsani inu zinthu izi. Ndipo ine ndikufuna kuti nditenge mutu, kuchokera mu mutu wa phunziro ili, kani, monga chonchi, *Dziko Kamodzinsu Likugawanika Pakati.*

<sup>28</sup> Ife tinali tikubwera kumusi dzulo, kapena madzulo apitawa, kudutsa ku Memphis, Tennessee, tinafika kumeneko mochedwerako masana, kapena gawo la madzulo. Ndipo ife sitimatha konse kudutsa mmisewu, a—ana ndi anthu anali atadzazana kwambiri. Ndipo ine ndinaganiza, “Kodi ichi chingakhale chiyani?” A—anthuwo sanavale ngati kuti anali ku msonkhano wachipembedzo monga mwina m'bale wathu wabwino, Billy Graham kapena Oral Roberts. Ndipo ine sindinaganize kuti iwo anali mu chigawo chimenecho pa nthawi imeneyo, mulimonse. Ndipo akazi anali atavala zazifupi, ndi ana aang'ono atawazungulira iwo, anali atangovala maovololo, ndi zina zotero, zophimba. Ndipo ndinali ndikudabwa chomwe izo zinali, ndipo potsiriza ife tinadzapeza. Iwo anali ndi—ndi kuguba kwa Santa Claus. Panali pali masauzande ambiri omwe ankawonera izo mmisewu, ndi zina zotero. Ndipo ife tinali ndi nthawi yovuta kwambiri kudutsa Memphis, chifukwa ikubwera nthawi ya Khristimasi.

<sup>29</sup> Ndipo Khristimasi limakhala tsiku lalikulu kwambiri la zamalonda, mpaka izo zangotsala pang'ono kuchotsa Kuperekamathokozo kunjja kwa chithunzicho, chifukwa . . . mu—mu dziko la malonda, mulimonse; chifukwa chakuti—dziko la zamalonda limakhudzidwa kwambiri ndi Khristimasi, chifukwa pamakhala anthu ambiri ogula. Ndipo iwo basi . . . Kuperekamathokozo ndi chongodutsa chaching'ono. Ndipo ife tikupeza, pamene tikuwona Khristimasi ikuyandikiranso, ine ndimaganiza icho chikanakhala chinthu chabwino kuti

tiyankhulepo pa phunziro ili, pamene ife tikuyandikira iyo. Kuwona kuti, kwenikweni, Khrisimasi sikuti. . .

<sup>30</sup> Ife timakondwerera tsiku ili la 25 Disembala pa kubadwa kwa Khristu, koma, ndithudi, aliyense amadziwa kuti ilo silinali tsiku lakubadwa kwa Khristu. Limenero linali tsiku la kubadwa kwa mulungu wa dzuwa wa Chiroma, limene pamene mpingo unatembenezidwiramo, kapena, kubweretsedwa mu Chikatolika, linakhazikitsidwa ku khonsolo ku Nicaea. Mmalo mwa ilo kukhala “mulungu wa dzuwa,” iwo analipanga ilo tsiku lobadwa la “Mwana wa Mulungu.” Pamenepo panali pamene, dzuwa, limayambira pa 20 mpaka. . . Ine ndikutanthauza pa 21 mpaka pa 25, ilo limakhala ngati mu lake. . . Ndayiwala dzina lomwe inu mumalitcha ilo, molondola. Ndi pamene ilo si kachiwiri kapena kawiri pamene ilo likudutsa pa siteji imeneyo. Ndipo ilo linali tsiku lobadwa la mulungu wa dzuwa, ndipo iwo anangotenga “Mwana wa Mulungu” ndipo analipanga ilo kukhala tsiku Lake lobadwa, kuti aliphatikize ilo ndi miyambo yawo yachikunja. Ndipo silimatanthauza, nkomwe, kukhala tsiku lobadwa la Khristu.

<sup>31</sup> Iye sakanakhoza kubadwa pa nthawi imeneyo, chifukwa Yudeya amakhala pafupifupi chimodzimodzi ndi pa—pa. . . pamwamba pa equator, monga ili liri, ndipo ife—ife tikupeza kuti, mu Yudeya, mu nthawi yachisanu, pa 25 Disembala, kumakhala mphepo ndi kuzizira. Azibusu sangakhale pa phiri, ndi zifukwa zambiri zomwe izo sizikanakhallira.

<sup>32</sup> Ndiyeno Iye anabadwa mwachirengedwe, monga chirengedwe china chonse, Iye—Iye anatulukira mu Kuphukira. Kawirikawiri ana a nkhusa amabadwa, mu Kuphukira; ndipo Iye anali Mwanawankhosa. Tsopano, ndikukhulupirira, Iye anabadwa, inemwini, Marichi, Epulo, kapena penapake cha pamenepo, kumayambiriro kwa Kuphukira.

<sup>33</sup> Koma ife tikupeza kuti iwo alipanga tsiku la malonda kuchokera pa ilo. Anthu kumadzazana m’misewu, ndi kugundana mapewa, ndi kumakangana pa zinthu, ndi kumadabwa za kumupatsa winawake mphatso, mtengo umene iwo ati adzalipirire pa izo.

<sup>34</sup> Tsiku lina, ine ndinadabwitsidwa. Pamalo amene ine ndinali nditayima, ndipo madona awiri anakamba zowapatsa abambo awo tsiku lobadwa. . . kapena mphatso ya Khrisimasi ya chaka chino. Ndipo mmodzi wa iwo anati, “Ine ndawagulira iwo botolo la kachasu.” Ndipo winayo anati, “Ine ndawagulira iwo paketi, kapena katonani ya ndudu,” kapena chinachake chonga icho. Ndipo iwo ankanena, mmodzi anapereka zochuluka motero za kachasu kuposa momwe iwo anachitira ndi ndudu.

<sup>35</sup> Ndipo ine ndinaganiza, “Ngati imeneyo si njira yake yoperekera a—a. . . kusinthana kapena kupereka mphatso mu



chikumbutso cha Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu!” Ndi chinthu chakupha bwanji icho chiri!

<sup>36</sup> Ndipo ine ndikuliwona dziko lathu liri mu chisoni monga momwe ilo liriri tsopano, layipitsidwa kuchokera mbali iliyonse, palibepo njira mdziko kuti ilo lidzabwereranso kwa ilo lokha kachiwiri. Kulibwino ife tisamalitse, zomwe tikuchita m’masiku ano. Pakuti ife tiri, pakali pano tikulira, za amodzi amatsoka aakulu kwambiri, ndipo—ndipo chimodzi cha zazikulu. . . Ife sitinkaganiza nkomwe kuti chinthu chimenecho chingadzachitike mu Amerika, koma icho chiri pano mulimonse. Ndipo kulekerera kwathu komwe pa Uthenga, iye wakhala wodwedwa ndi mphutsi ndi zinthu zoterozo, ndipo zikhala zikuipirayipira. Palibe kukayikira nkomwe, mmalingaliro anga, koma kuti izo zikhala zikuipirayipira mopitirira.

<sup>37</sup> Koma ife tikupeza, pa Khrisimasi iyi, kuti tifike ku phunziroli, kuti Khrisimasi iyi yalipeza dziko lapansi monga momwe ilo linkachitira zaka thuu sauzande zapitazo, pamene Yesu anabwera. Izo sizinasinthe kwambiri kuyambira pamenepo. Chifukwa, iyi, Khrisimasi imeneyo inalipeza dziko likugwa, ndipo ankafunafuna Mesiya kuti athandizire kuligwirizira ilo pamodzi. Ndipo—ndipo umo ndi momwe izo ziliri lero, ife tikuchita chinthu chomwe chomwecho. *Dziko Kamodzinsu Likugawanika Pakati.*

<sup>38</sup> Tsopano, izo si kuno kokha ku Amerika, koma izo ziri konsekonse mdziko, kulikonse kumene inu mungapiteko; dziko lachipembedzo, dziko la ndale, chirichonse, a—dziko la makhalidwe abwino. Ilo—ilo, palibenso zochuluka za izo, ndizo basi. . . Makhalidwe angokhala pakati pa anthu abwino, osatinso, ndipo ndi zovuta kwambiri kuzipeza. Izo ndi—ndi zamanyazi. Ndipo ndale ndi chirichonse zavunda, mpaka chinthu chonsecho chikudwala ndi zilonda zonunkha, kuyambira kumutu mpaka kumapazi, dziko lonse. Kachitidwe kathu ka ndale, kachitidwe kathu kachipembedzo, kachitidwe kathu ka makhalidwe, chirichonse chimene ife tiri nacho, chapita! Basi, palibe njira yosungira izo pamodzi. Ilo, ilo latha! A. . . Ife tiri kumapeto kwa ulendo. Ndizo zonse zomwe ziripo kwa izo.

<sup>39</sup> Ife, ine ndikudziwa ife tayankhula za izo nthawi yayitali, koma limodzi la masiku awa izo zidzakhala zitadutsa kuzikamba, icho chidzakhala chinthu chambiri yakale, ndipo tidzazipeza tokha kunja ngati ife sitiyang’ana pa nthawi ino.

<sup>40</sup> Ine ndikudabwa, ngati ife Khrisimasi iyi, ngati Mulungu ayenera kumutumizanso Iye monga Iye anachitira kumbuyo uko zaka thuu sauzande zapitazo, ngati Iye angamutumize Iye kwa ife mu 1964, ine ndikudabwa ngati ife sitingachite ndi Iye monga iwo anachitira nthawi imeneyo? Ine ndikungodabwa ngati Kudza Kwake kungakhale chirichonse, Iye angalandiridwensu

nkomwe, mu—mu—mu dziko la ndale kapena mu dziko lachipembedzo, kuposa momwe Iye analiri nthawi imeneyo? Ine ndikungodabwa ngati ife tiri mu mawonekedwe enanso kuti timulandire Iye, monga Iye anali nthawi imeneyo? Koma ife tikudziwa kuti Iye anakanidwa nthawi imeneyo.

<sup>41</sup> Kodi ife tingachite chiyani kwa Iye ngati Iye angabwere? Mwinamwake dziko lachipembedzo, limene ine ndikukhazikitsirapo izi, lingachite kwa Iye monga linachitira nthawi yina. Iwo angamupachike Iye ngati iwo angathe, (iwo sanasinthe), pa chifukwa chomwecho chimene iwo anachita nthawi yinayo.

<sup>42</sup> Nchifukwa chiyani iwo anachita izo, kodi iwo anamupachika Mmodzi yemweyo amene iwo ankamupempherera kuti abwere pa dziko lapansi, kuti adzawapulumutse iwo, kuti adzawachotse iwo mu chipwirikiticho? Iwo anapachika chiyembekezo chokhacho chimene iwo anali nacho. Chifukwa chiyani? Nchifukwa chiyani iwo anachita zimenezo? Chifukwa, pamene Mulungu anayankha pemphero lawo, Iye anayankha ilo mwanjira imene iwo sankayembekezera kuti lingayankhidwire. Pamene Iye anabwera, Iye sanabwere konse mu kukoma kwa zaumulungu zawo.

<sup>43</sup> Ndipo ngati Iye angabwerenso, lero, Iye angabwere mwanjira yomweyo; kunjira kwa kukoma kwa dziko lapansi kapena fioloje ya tchalitchi, ndi momwe iwo akanati aganizire za Iye. Iye nthawizonse amabwera. Monga anthu a Mulungu, pamene iwo alowa mu vuto, ndi kupemphera, ndiye Mulungu amawapatsa iwo chimene iwo akuchipempherera, koma Iye amapereka izo mwanjira yomwe ili yabwino kwa iwo. Ndipo iwo anawakana Iwo, chifukwa Iwo sanabwere momwe iwo akuganizira kuti Iwo akanabwerera. Iwo anawakana Mawu odzozedwa a Mulungu, ndipo Iye ndi Mawu.

<sup>44</sup> Tsopano, Mulungu, mu mibadwo yonse, nthawi zonse, pamene Iye ayamba, “Pamene Iye ankayankhula Mawu Ake mu nthawi zamakadzana zinali kudzera mwa aneneri, mmasiku otsiriza ano kudzera mwa Yesu Khristu, Mwana Wake,” ife tikupeza kuti uliwonse wa mauneneri amenewo unali woti udzagwirizane ndi m’badwo winawake. Monga Mfumu Nebukadinezara pamene iye analota loto ili, ndipo dziko la Amitundu kuyambira kumutu mpaka kumapazi, ndipo Daniele anapereka kumasulira kwa loto ili; kuti unali—ulosi ku dziko lonse lapansi, kwanthawizonse, gawo lililonse la Ufumu wa Amitundu, monga ilo likanamabwerera kuchokera kumutu mpaka kumapazi. Ndipo aneneri nthawizonse akhala akuyankhula Mawu amene akuyenera kudzachitika mu m’badwo uliwonse. Ndipo pamene Mulungu . . .

<sup>45</sup> Anthu akalowa mu vuto, ndipo Mulungu amawayankha iwo. Iye amawatimizira iwo mneneri wodzozedwa kapena mtundu

wina wa mtumiki, chifukwa Iye sangabwerere mmbuyo pa Mawu Ake amene Iye anawakonzero ku m'badwo umenewo. Koma, chimene Iye amachita, Iye amamutumiza mtumiki kuti akapangitse gawo limenelo la Mawu kukhala moyo ku m'badwo umenewo. Nthawizonse amachita zimenezo, mwaona. Iye anawapanga Mawu Ake pachiyambi. Iye ankadziwa mapeto kuchokera pachiyambi. Iye anawayankhula Mawu Ake. Ndipo m'badwo uliwonse, pamene iwo alowa mu vuto, iwo anka . . . iwo ankapemphera, ndipo Mulungu ankatumiza wodzozedwayo. Ndipo wodzozedwayo mwamtheradi ankalipangitsa lonjezo limenelo la m'badwo umenewo, lomwe linanenedweratu kwa m'badwo umenewo, kukhala moyo. Ndipo ndicho chimene Iye amachita nthawi zonse. Mulungu samasintha dongosolo Lake. Tsopano, ife sitimapeza konse Mulungu akusintha.

<sup>46</sup> Mulungu anazikhazikitsa izo nthawi imodzi, momwe Iye akanati adzamupulumutsire munthu, amene anali mmunda wa Edeni, pansi pa magazi okhetsedwa. Ife tayesetsa kachitidwe kena kalikonse, kuyambira ku masamba a mkuyu mpaka ku maphunziro, kuweringa maganizo, zipembezoz za kachitidwe, ndi zina zotero, ndipo chidutswa chirichonse cha izo cha—chakanidwa; ndipo izo sizinagwirepo konse ntchito, izo sizidzagwira konse ntchito. Mulungu adzakomana kokha ndi munthu pansi pa Magazi okhetsedwa, ndipo ndiwo malo okhawa amene Iye ati adzakomane naye iye, chifukwa limenelo linali lingaliro Lake loyamba. Iye sadzakumana konse ndi munthu pansi pa mtundu uliwonse wa dongosolo lamakhalidwe abwino. Iye sadzatero konse, sizidzatheka mdzikoli! Mungobwerera ku Njira ya Mulungu, ndicho chimene Iye ananena poyambirira. Ndipo Iye ndi wopandamalire, sangasinthe, ndipo nthawizonse Iye amakhala yemweyo. Pamenepo ndi pamene Iye amakomana ndi munthu, ndipo apo pokha. Ndi chifukwa chake ife timalephera kukhala ndi chiyanjano lero, ndi chifukwa chake mpingo uli wogawanika kwambiri, chifukwa aliyense ndi wogawanika mu kachitidwe, ndipo, pamene iwo achita zimenezo, ndiye Mulungu amawakana iwo, apo pomwe. Iye akufuna ife kuti tizikomana pansi pa Magazi, pamene tizikhala ndi zinthu zonse mofanana, pansi pafupi ndi Mtanda. Cholinga chokhacho cha Mulungu chochitira izo! Mulungu nthawizonse amatumiza Mawu Ake.

<sup>47</sup> Ndipo ife tikupeza, lero, kuti dziko lero liri chimodzimodzi basi monga momwe linali mu tsiku limenelo; likudzipeza lokha, kachitidwe kake ka ndale, ndi zina zotero, zonsezo zikugwa, ndipo likuyembekezera mesiya amene ati adzalizgwirizanitse ilo pamodzi.

<sup>48</sup> Tsopano, mawu akuti *mesiya* amatanthauza “wodzozedwayo,” chinachake chodzozedwa. Mulungu! *Ili* ndi vumbulutso la Yesu Khristu, Bukhu lonselo linasindikizidwa ndi Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri za vumbulutso la Yesu Khristu.

Yesu Khristu anali mu Genesis; Yesu Khristu anali pakati pa Bukhu. Yesu Khristu anali mu—mu Eksodo ndi Genesis, ndipo Iye anali pakati pa Bukhu ndipo Iye anali mu—Chipangano Chatsopano, ndi mu Chivumbulutso ndi mpaka ku mapeto, “yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse.” Zonsezo ndi Mulungu!

<sup>49</sup> “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.”

<sup>50</sup> “Mulungu mu nthawi zamakedzana ndi munjira zosiyanasiyana ankalankhula kwa makolo kudzera mwa aneneri.” Pamene Mawu a Ambuye amabwera kwa aneneri, ndipo iwo okha, chifukwa iwo ankadzedzwa ndi Mawu, iwo anali ndi ufulu wotanthauzira Mawu. Ndipo Mulungu ankagwira ntchito kudzera mwa iwo, kutsimikizira kuti Mawu anali olondola. “Ngati ine. . . pangakhale wina pakati panu amene ali wauzimu, kapena mneneri, Ine Ambuye ndidzadzizindikiritisa Inemwini kwa iye. Ndipo ngati chimene wanena chichitika, ndiye mumvereni iye. Ngati izo sizichitika, musamumvere iye.” Izo sizoposa kulingalira kwabwino, kwa munthu aliyense.

<sup>51</sup> Tsopano ife tikudzipeza tokha pano, mmasiku otsiriza tsopano, pamene ife tikuyembekezera Kudza kwa Ambuye kenanso.

<sup>52</sup> Chabwino ndikukumbukira mlaliki wakale wa Chibaptisti amene anandibatiza ine mu Dzina la Yesu Khristu, pamene ine ndinali mnyamata wamng’ono chabe. Ndipo iye anakonda kukambirana nane phunziro ili, la Yohane M’batizi. Iye anati, “M’bale Billy,” iye anati, “pamene Yohane. . . Pamene Iye anati, ‘Balola kuti izo zikhale chomwecho,’ ndipo kenako iye anamulolera Iye.” Iye anati, “Kenako Yohane, anamubatiza. . . Yesu anamubatiza Yohane, chifukwa ife tikudziwa kuti Yohane anali asanabatizidwe, ndipo komabe iye ankalalikira ubatizo.” Chabwino, izo nthawizonse zinkakhala ngati zimandidodometsa ine, pang’ono.

<sup>53</sup> Ndiye kuno osati kale kwambiri, izo zinawululidwa kwa ine, pa njira iyi, kuti pamenepo anakumana mu dziwe limenelo, mu dzenje lija la madzi, atumiki awiri aakulu kwambiri amene dziko linayamba lawawonapo: a—mwamuna amene anali pamwamba pa aneneri onse, amene anali Yohane, “panalibe konse munthu wobadwa mwa mkazi, wamkulu monga iye”; ndipo pamenepo panali Mulungu, Iyemwini, akuwonetseredwa mu thupi la mnofu. Ndipo kumbukirani, ndipo Baibulo limatiuza ife kuti, “Mawu a Ambuye amadza kwa mneneri.” Ndipo pamene Mawu anasandulika thupi; apa panayima mneneri mmadzi. Ndipo Mawu ndi mneneri anabwera pamodzi, iwo anadziwana wina ndi mzake! Kulondola. Mawu Iwoeni, atapangidwa thupi, Mwana wa Mulungu mu thupi, anadza kwa mneneri, mmadzi.

54 Mneneri anati, “Ine ndikuyenera kubatizidwa ndi Inu, ndipo Inu mukubwereranji kwa ine?”

55 Iye anati, “Balola kuti izo zitero, pakuti kuyenera kwa ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse.”

56 Zindikirani! Yohane, pokhala mneneri, anadziwa kuti Iye anali Nsembe. Ndipo nsembeyo ikuyenera kutsukidwa isanaperekedwe ngati nsembe. Ndipo ndi chifukwa chake Iye ankayenera kuti abatizidwe.

57 Oh, lero, zikuyenera kwa ife, kuti ife tikwaniritse chirungamo chonse cha tsiku lathu. Ora liri pano. Baibulo likutiya ife zimene zidzachitike mu tsiku lino. Ife tikudziwa chimene Baibulo limanena kuti chidzachitika mu tsiku lino. Ziri kwa ife kuti tigwiritsitse kwa Mulungu mpaka zinthu izi zitachitika. Ndi oralo! Pemphererani wodzozedwawo amene ati adzatipatse ife chipulumutso chimene tikuchiyembekezera, chifukwa Mulungu analonjeza zimenezo.

58 Iwo anawakana Mawu odzozedwa a Mulungu nthawi imeneyo, ndipo atatero ilo linagwa, linagawanikana pakati. Ndipo kamodzinsu ife tikuzipeza, pa nthawi ino, ilo likugawanika pakati kamodzinsu. Ine ndikupeza, monga ine ndinanenera, ndale zathu zavunda, moyo wathu wa mpingo wavunda. Chachitika ndi chiyani? Nazi zomwe zinachita izo; pamene inu muchokapo, nthawi iliyonse, kutalikana ndi dongosolo la Mulungu, inu mudzapeza chivundi. Izo sizingakhoze kuyima. Mawu a Mulungu ndi osalephera, ndipo palibe chinthu china chimene chidzatenge malo Ake, sichingakhoze konse.

59 Kachitidwe kathu ka maphunziro, kachitidwe kathu ka chipembedzo, zatenga malo a Mzimu Woyera kutsogolera mu tchalitchi. Kuphunzitsa kwathu kwakukulu kwa azitumiki ndi zinthu zatenga malo a—a mapemphero a usiku wonse, ndi njira yanthawi zakale imene ife tinkafikira kwa Mulungu. Tsopano, mmalo mokhala ndi alaliki, ife tiri ndi anamatetule, amuna odziwa Mawu chimodzimodzi basi, iwo akhoza kukhala pamenepo ndi kuwayika Iwo pamodzi mwanjira yakuti izo zimadodometsa momwe iwo angachitire izo. Iwo amadziwa zimango, koma izo si Zimphamvu. Ife tikufuna Zimphamvu. Ine sindikusamala za zimango; ndikufuna kudziwa Zimphamvu. Kodi Izo zimachita chiyani?

60 Sindikudziwa momwe galimoto iyo imayendera kunja uko. Iyo imakhala ndi mapistoni ndi masilinda, ndipo sindikudziwa kuti imagwiritsa ntchito mphamvu yochuluka bwanji. Chinthu chokhacho chimene ine ndikuchidziwa ndi zimphamvu, zimaiyika iyo kunja uko ndi kumaiyendetsa iyo.

61 Ndizo zimene ife timazidziwa, Mulungu anapanga lonjezo, “Ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa mnofu wonse, ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera.” Kodi Iye adzachita izo

motani? Ine sindingathe kukuuzani inu. Ine ndikungofuna ku dziwa Zimphamvu za dongosolo la Mulungu. Ndicho chinthu chofunikiracho.

<sup>62</sup> Lero taphunzira zimango mpaka izo zonse ndi zimango. Ndi yaubwino wanji galimoto yopanda kanthu mkati mwake kuti iyendetse iyo? Kodi awubwino wanji magetsi ngati—ngati a...kapena zoyikamo, ngati mulibemo mphamvu yoti ilowe mmenemo? Mwaona, ife tiri nazo zimango zonse, ife tiri nawo masukulu ndi aphunzitsi, ndi zina zotero, omwe angamuphunzitse munthu, mpaka iye atha kuyima pa guwa ndi makhalidwe amenewo mpaka nkukhala munthu wokutha kuyankhala. Izo sizibweretsabe Mphamvu ya Mulungu. Ili kuti Mphamvu ya Mulungu yomwe inali ya kwa mpingo? Uli kuti Mdalitso wa chipentekoste umene unkayenderera kudutsa mmatchalitchi? Ndi chifukwa chake dziko lathu likugawanika pakati, chifukwa tachoka ku mfundo zenizeni za Mulungu, ndipo tawaphunzitsa amuna mu machitidwe ndi zinthu. Ndipo ndizo zomwe zatifikitsa ife mu chochitika chomwe ife tirimo lero. Ine ndikukhulupirira kuti ndicho chifukwa dziko lathu likugawanika pakati.

<sup>63</sup> Zochitika izi zakhala ziripo padziko lapansi kuyambira masiku a Nowa. Ife tikupeza pamene Mulungu...anali ndi Nowa, mneneri wa chirungamo, akupita ndi uthenga wake, panali chochitika cha chisembwere mu tsiku limenelo, monga Baibulo linanenera, “Kudya, kumwa, kukwatira, kuperekedwa mu chikwati.” Ife tikupeza kuti, kususuka ndi zachisembwere, ndi zina zotero, zinkachitika mu tsiku limenelo. Ndipo kenako dziko linagawanika pakati chifukwa anthu anawukana uthenga wa Mulungu, wa tsiku limenelo. Nowa anali mneneri wodzodzedwa ndi Mulungu, wotumidwa ndi Mulungu, wokhala ndi uthenga wochokera kwa Mulungu, ndipo iye anawachenjeza anthuwo chiweruzo chisanabwere. Ndipo iwo ananyogodola ndi kuseka, ndi kuzisereula izo, ndi kunyoza, ndipo kachitidwe konse ka dziko kanagawanika pakati, mu tsiku limenelo, ndipo iwo anamizidwa pansu pa nyanja. Zoona zimenezo. Chifukwa chiyani? Iwo anawukana uthenga wa oralo.

<sup>64</sup> Ife tikupeza kuti chinthu chomwecho chinachitika mu Igupto, pamene Mose anawatsogolera ana a Israeli kuti atuluke. Dongosolo lonse la Aigupto linali litavunda. Ndipo ife tikupeza tsopano izo zinachitika kachiwiri, pamene Mulungu anatomiza mtumiki wodzozedwa kumeneko chifukwa cha Mawu Ake. Kunali kuti akakwaniritse Mawu Ake.

Inu mukuti, “Kodi kunali kuti akakwaniritse Mawu Ake?”

<sup>65</sup> Iye anamuuzza Abrahamu kuti ndicho ndendende chimene Iye akanati adzachite. Ndipo pankayenera kuti padzakhale wina adzabwere pa chochitikacho, pa nthawi imeneyo, kuti adzawapangitse Mawu amenewo kukhala moyo pamaso pawo

pomwe. Mulungu anali atamutumiza Mose Wake kumeneko, ndipo, chinthu chomwecho chimene Iye analonjeza kuti adzachita, iye anachichita icho, chifukwa iye anali Mawu odzozedwa a ora limenelo. Iye anati izo zikanadzaliweruza dziko limenelo. Mawu a Mulungu anati, “Ine ndidzaweruza fuko limenelo ndi zopambana, zodabwitsa zamphamvu ndi zizindikiro.”

<sup>66</sup> Apo panayima mwamuna, munthu wamba chabe ngati inu kapena ine, analandira Mawu kuchokera kwa Mulungu, ndipo anapita kunja uko ndipo anayankhula chirengedwe kuti chikhalepo. Anati, “Mulole . . .” Anatenga mchenga, ndipo anati, “Mulole utitiri ubwere kuchokera mnthaka.” Ndipo Mawu a Mulungu, kudzera pakamwa pa mneneri ameneyo, pokhala kuti anali mu ora lomwe amayenera kukhalamo, utitiri unaphimba dziko lonse. Iye anaphimba dziko ndi achule, ndi nsabwe. Iye anaphimba ilo ndi mitundu yonse ya—ya mliri ndi zinthu. Chifukwa, Mulungu anapanga lonjezo, ndipo ora linali pamenepo kuti ilo lidzozedwe, Mawu odzozedwa a ora limenelo limene iwo akukhalamo.

<sup>67</sup> Ndicho chimene ife tikuchisowa lero, sikubwerera ku kachitidwe ka seminare kena, koma Mawu odzozedwa a ora limene ife tikukhalamo, kuti timubweretsenso Yesu Khristu kwa dziko kachiwiri. “Yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Pali a—pali dongosolo limene linaikidwira tsiku lino, lonjezo la Mulungu. Ndipo njira yokhayo yomwe ife tidzakhoze konse kukhala bwino, ndi kulola Mawu amenewo kuti adzozedwe. Uko nkulondola. Zakhala zikuchitika nthawi zonse. Inde.

<sup>68</sup> Ife tikupeza kuti kuyipitsidwa kwakukulu kwa makhalidwe mmasiku a Nebukadinezara. Iye anali ndi munthu wodzozedwa. Pamene cholembedwa cha dzanja chinabwera pa khoma, Iye anali ndi munthu amene ankatha kuwerenga izo.

<sup>69</sup> Masiku a Loti ndi Sodomu, ife tikupezanso dziko likugawanika pakati. Mulungu anapulumutsa chimene chikanakhoza kupulumutsidwa, kuchokera mwa ilo.

<sup>70</sup> Mmasiku a Yesu Khristu, ife tikupeza kuti kachitidwe kopangidwa ndi munthu kanali katalitengera dziko mu chikhaldidwe choterocho, ndi ndale zawo za tsiku limenelo, mpaka, iwo, dziko lonse linali likugawanika pakati, pa Khristimasi yoyambirira.

<sup>71</sup> Tsopano ife tachita chinthu chomwecho, tatembenukira mmbuyo mozungulira ndipo tawaipitsa Mawu a Mulungu, mwa kachitidwe ka chipembedzo, mpaka ife tikulipeza ilo likugawanika pakati. Ndi kachitidwe kamodzi kati kamene ife tingakadalire tsopano? Ndi kachitidwe kati kamene ife tingapiteko, kachitidwe ka Methodist, Baptisti, Presbateria, kapena Pentekoste? Palibepo kalikonse nkomwe kamene ife tingachite koma kubwerera ku Mawu odzozedwa a lonjezo la

ora lino. Kachitidwe aka ndi kofooka, ndi kofota. Iko, iko ndi, iko ndi kachitidwe kopangidwa ndi anthu, ndipo iko sikadzakupulumutsani inu. Mulibemo Moyo mwa iwo. Moyo wokha uli mu Mawu a Mulungu. Iwo ndi Moyo. Iye ananena chomwecho.

<sup>72</sup> Ndipo momwe zinkakhalira nthawi imeneyo, pamene iwo ankapemphera, anthu anazipeza okha ku mapeto a ulendo wawo, kapena kumapeto a zingwe zawo, monga momwe zinali mmasiku a Nowa ndi mmasiku a Mose, ndi zina zotero. Pamene iwo anadzipeza okha, kuti sangathe kupita patsogolo paliponse, ndiye iwo anayamba kupemphera. Ndipo pamene anayamba kupemphera, Mulungu nthawizonse amayankha. Kenako Yesu anadzabadwa.

<sup>73</sup> Dziko pa nthawi imeneyo, monga ine ndinanena, linali likugawanika pakati. Fuko lililonse linkafunafuna mesiya, chimodzimodzi monga momwe tikuchitira lero. Roma ankafunafuna munthu wanzeru kwambiri amene akanatha kubwera pakati pawo, a—munthu wamkulu amene anali ndi njomba zonse zankhondo, kuti iye akanakhoza kupita kumeneko ndi kukagonjetsa Greece ndi dziko lonse. Greece ankafunafuna chinthu chomwecho, winawake amene akanawauza momwe angaligonjetsere dziko lonse lapansi.

<sup>74</sup> Dziko lachipembedzo cha Chiyuda panthawi imeneyo linkafunafuna wamkulu wa asilikali. Iwo ankaganiza kuti akanadzabwera Mesiya kuchokera Kumwamba, ali ndi ndodo yayikulu yachitsulo mmanja mwake, ndipo Iye akanadzamugwetsera Roma pansu, kuwapondereza iwo ndi kuwathamangitsira iwo ku nyanja. Ndipo onse kumeneko, iwo ankafunafuna munthu wa mtundu umenewo. Iwo ankamufuna mkulu wa asilikali.

<sup>75</sup> Monga zochulukana zonse monga zipembedzo zathu za lero, zipembedzo zathu zikufunafuna munthu wapamwamba. Fuko lathu likufunafuna munthu wapamwamba. Russia ikufunafuna munthu wapamwamba. Dziko la- kummawa likufunafuna mmodzi. U.N. ikufunafuna mmodzi. Mipingo ikufunafuna mmodzi. Koma ndi mtundu wanji wa mmodzi amene iwo akumufunafuna?

<sup>76</sup> Russia ikufunafuna mesiya amene ali wodzozedwa ndi—ndi ubongo amene amadziwa kuwagonjetsa iwo mu danga lakunja, kukamumenya aliyense mpaka ku mwezi. Iwo akufuna kugonjetsa dziko. Ndizo basi. . .

<sup>77</sup> Koma, inu mwaona, pamene iwo afunsa zinthu izi, ndi kupempha izi, iwo samafunsa monga Yesu ananenera. Ife timayesetsa kumupanga Mulungu monga a—ngati mnyamata womutuma, “Ambuye, mundichitire ine *ichi!* Ndipo Inu mundichitire ine *ichi!* Ndipo Inu mupite mukachite *icho,*” kumuza Iye choti achite.



78 Yesu anati, “Pamene mupemphera, pempherani motere, ‘Atate Athu Amene Muli Kumwamba, Dzina Lanu liyeretsedwe. Ufumu Wanu udze. Kufuna kwanu kuchitidwe.’” Ndani, mupeze kumene timachita zimenezo? Nthawizonse timafuna kuti Mulungu azitichitira ife zinthu, kapena kutichitira ife chinachake. Koma pamene ife tikhala ololera kunena, “Kufuna kwanu kuchitidwe,” kudzipereka tokha kwa Iye, kupereka njira zathu kwa Iye. Zonse zomwe ife tiri, kuzipereka izo kwa Iye. Pamenepo ndi pamene Mulungu adzasunthe, pamene inu mukulolera kuti Iye agwire ntchito pa inu, osati inu kugwira ntchito pa Iye.

79 Kumulola Iye akuuzeni inu, osati inu kumuuza Iye ndi kuzipotoza izo mozungulira. “Bwerani ku kachitidwe kathu, O Ambuye Mulungu, tipangeni ife tonse Amethodisti, tonse a ife Achipentekoste, tizilamulira pa ena onsewo. Ife tikufuna namandwa, ife anthu Achipentekoste, ife Amethodisti ndi Abaptisti.” Ife tiri ndi maseminare, tikumanga zazikulu zikulu, nkumati, “A—mapeto a nthawi ali pafupi, Kudza kwa Ambuye,” tikumanga maseminare a mtengo wa madola mamillioni, ndi zina zotero. Kuyesetsa kutani? Kutipezera ife mesiya. Uko nkulondola.

80 Ambuye angodzutsa chinachake kwinakwake, chipembedzo chirichonse chiwatengera iwo mmodzi wa mtundu womwewo. Ndizo ndendende. Fufuzani. Penyani pamene machiritso Auzimu anabwerapo, ndi ochiritisa Auzimu angati? Aliyense ankayenera kukhala mchiritisi Wauzimu.

81 Analipo Mose mmodzi mmasiku a kutuluka kumeneko. Panali Eliya mmodzi, Elisha mmodzi, Yesaya mmodzi, ena otero.

82 Tsopano ife tikupeza kuti dziko likufuna mesiya wawo wawo. Russia akufuna wawo, ndipo United States akufuna wawo, dziko la mpingo likufuna wawo. Aliyense akufuna mesiya wakewake, koma iwo akufuna izo mwanjira imene—imene iwo akhoza kulamulira izo. Iwo akufuna kukhala ndi ulamuliro pa mesiya ameneyu. Oh, ndithudi. Eya, iwo, ngati iwo akanatero. Ngati Mulungu akanawatimizira iwo mwa kufuna kwawo, ndithudi iwo akanavomereza izo. Koma inu mukuona, kenako, Mulungu ankadziwa zosowa zawo. Iye, Iye sanalonjeze kuti adzatitimizira ife zofuna zathu ndi zomwe ife tikupempha, koma zosowa zathu.

83 Iwo ankafuna wamkulu wa asilikali; iwo analandira Mwana. Mwaona, ndicho chimene iwo ankasowa. Iwo ankasowa mwana (chiyani?) kuti adzawatsitse iwo, kuti adzawachepetse iwo.

84 Ndicho chimene mpingo wodzinenera wokha ukusowa lero, kudzichepetsanso wokha kachiwiri. Zafika pa malo, akuti palibepo kulapa ndipo palibepo chikondi pakati pa anthu. Zikuwoneka ngati zikufa tsiku ndi tsiku. Mpingo ukuzirala.

Kulikonse, inu mukupeza kuti chitsitsimutso chatha, ndipo inu mukupeza ukuzirala. Ife tikusowa kutsitsidwa. Ndipo ife . . .

<sup>85</sup> Iwo anapempha mkulu wa asirikali; ndipo anapeza Mwanawankhosa. Chifukwa chiyani? Ndizo, Mulungu ankadziwa chimene iwo ankasowa. Ndicho chimene iwo ankasowa. Iwo ankasowa Mpulumutsi. Iwo ankaganiza kuti anapulumutsidwa, koma Mulungu ankadziwa kuti iwo anali asanatero.

<sup>86</sup> Ndipo ndicho chimene dziko likusowa lero, kachiwiri, ndi Mpulumutsi, Mpulumutsi wa chikhalidwe ichi, chinachake chomwe chingagwire ilo pamodzi. Osati ulamuliro wa maphunziro, mtundu wina wa kachitidwe ka makina, kapena mtundu wina wa kachitidwe ka maphunziro. Chimene ife tikusowa ndi Mphamvu ya Ambuye Yesu Khristu, ndi chisomo chopulumutsa, kubwerera mu mpingo kachiwiri, pamene amuna, akazi, anyamata, ndi atsikana, akhoza kupulumutsidwa.

<sup>87</sup> Kodi ife tadikirira motalika kwambiri? Kodi alipo ambiri kunja uko omwe sadzalowamo konse? Kodi dzina lotsiriza lawomboledwa? Kodi ndiro lomwe liri vuto lero? Izo zikhoza kukhala, inu mukudziwa. Inu mukudziwa, izo—zikhoza kukhala zophweka, ndipo osasokoneza Malemba, nkomwe. Izo zikhoza kukhala. Chotero, ife sitikudziwa tsopano, tiyeni tikhale osamalitsa.

<sup>88</sup> Koma iwo ankaganiza kuti anapulumutsidwa, ndipo—ndipo, koma Mulungu ankadziwa bwinoko kuposa momwe iwo ankachitira. Ndipo chinthu chomwecho chikuchitika lero.

<sup>89</sup> Iwo anali atawatenga Mawu amene Mulungu anawapatsa iwo a tsiku limenelo, amene iwo ankayenera kuti adziwe tsiku limene Iye anali kudza, ndipo anali atapanga mwambo kuchokera mwa Iwo. Yesu anati, “Inu mwawatenga Mawu a Mulungu ndipo mwawapanga Iwo kukhala opanda mphamvu, ndi miyambo yanu.”

<sup>90</sup> Ndicho chinthu chomwecho chimene chachitika lero mu kachitidwe kathu, mdziko la kachitidwe ka chipembedzo. Kachitidwe ka mdziko kawatenga Mawu a Mulungu ndi kuwapanga Iwo mwambo. Ndipo ndicho chifukwa chake Iwo alibe mphamvu iliyonse mwa Iwo. Palibe chirichonse chimene chiti chidzatuluke mwa Iwo, chifukwa Iwo asakanizidwa.

<sup>91</sup> Inu simungayike chimanga chenicheni mu chinachake chimene sichiri, pokhapokha itakhala nthaka, ndipo icho sichingamere. Inu mukhoza kuchiyika icho padzuwa ndi kuchisiya icho chizitenthedwa, inu mukhoza kuchita chimene inu mukufuna, koma icho chimatengera mtundu winawake wa nthaka. Icho chikuyenera kukhala mmenemo. Icho chikuyenera kukwiriridwa. Icho chikuyenera kukhala pansa pa chikhalidwe choyenera, kuti icho chimere.

<sup>92</sup> Ndipo chomwechonso amatero Mawu a Mulungu! Inu simungawutenge mpingo ndi kuwubweretsa iwo ku moyo, pa mwambo wina. Inu mukhoza kukhala ndi mamembala, mwa mamillioni, koma inu simudzatha konse kutsitsira pansi Mphamvu ya Mulungu mpaka ife titabwerera ku Mawu apachiyambi kachiwiri, kubwerera ku Mawu a maziko, kubwerera ku Magazi, kubwerera kwa—Yesu Khristu, kubwerera ku misonkhano ya mapemphero akachitidwe-kachikale, ndi kubwerera kwa Mulungu! Ife tikhoza kukhala kuti tinapita kutali kwambiri, tsopano, kuti ora lapita. Koma, mulimonse, Uthenga ukuyenera kulalikidwa. Ife sitikuyenera kuweruza izo.

<sup>93</sup> Mulungu ankadziwa chimene iwo ankasowa, chotero Iye anawapatsa zomwe iwo ankazisowa. Chotero kachiwiri, ife tikupeza, zomwe iwo anali nazo, ife tachita chinthu chomwecho.

<sup>94</sup> Russia ndi ena onse a iwo akufuna zawo. Ndipo asayansi osiyanasiyana akufuna kudzipangira dzina lalikulu. Fuko lirilonse likufuna kupeza munthu wake wanzeru. Ife tikufuna wathu. Ife tikufuna kachitidwe ka maphunziro mmenemo. Ife tikufuna zachipembedzo. Ndizo ndendende basi zomwe ife tiri nazo. Ndi zomwe inu munachita. Ndi zomwe inu munkafuna, ndi zomwe Mulungu anakupatsani inu. Tsopano kodi inu muchita nazo chiyani mukakhala nazo izo?

<sup>95</sup> Ife tikuyankhula za Russia kwa miniti ina. Aku Russia akufunafuna munthu yemwe angagonjetse mu mlengalenga. Iwo akuwaphunzitsa iwo mofulumira momwe iwo angathere, asayansi awo. Bwanji ngati iwo atampeza mmodzi, nanga bwanji ngati angampeze mesiya wawo, kodi ife tichita chiyani? Ndipo chifundo pa ife ngati iwo angapeze izo! Kumbukirani, Germany anampeza mesiya woteroyo osati kale, osati kale kwambiri, Hitler. Ndipo ife tikudziwa chimene icho chinachita kwa iwo.

<sup>96</sup> Tsopano nanga bwanji mpingo, ndi mesiya wa mtundu wanji yemwe mpingo ukumuyembekezera, lero? Inu, mpingo, walira mokweza kwambiri. Chotero, kodi ife tikufuulira chiyani za mesiya, kodi ife tikufuulira chiyani? “Chitsitsimutso mu nthawi yathu! Kubwerera ku *ichi*, *icho*, ndi *chinacho*.” Kodi iwo akufunafuna chiyani, kuti adzachite izo? Kodi mukufunanso chiyani? Kodi mpingo ukufuna chiyani, mulimonse?

<sup>97</sup> Ife tachipeza kale Icho! Mulungu anapereka Icho kwa ife. Ndi lonjezo Lake la ora lino. Ife timayang’ana mu Baibulo, timaziwona izo paliponse mu Baibulo. Odzozedwa anabwerapo ndipo anadzawapanga Mawu amenewo kukhala amoyo kachiwiri, mu ora lomwelo la ora limenelo. Ndipo tiri naye Mesiya. Uyu ndi Iyeyo, Mawu! “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu.” Ndipo Mawu akanali Mulungu, Ahebri 13:8, “Yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Ife tikudziwa zomwe zikuyenera

kuchitika mu tsiku lino. Ife tikufuna Mesiya. Ndipo Mulungu anatipatsa ife Mesiya, Mawu Ake olonjezedwa a tsiku lino. Iwo akungoyembekezera winawake wa chikhulupiriro, kuti awadoze Iwo ndi kuwapanga Iwo kukhalanso amoyo. Inde, bwana. Iwo ndi Mesiya weniweni, Iwo ndi Mawu a Mulungu. Chomwe, Yesu anati, “Zonse kumwamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Mawu Anga sadzachoka konse.”

<sup>98</sup> Koma mpingo ukukhala wakufa mwauzimu, wapita, ora lawadutsa iwo. Iwo ali mu kugwa, ndipo sakudziwa nkomwe choti achite, wina akuthamangira njira *iyi* ndipo wina njira *yo*. Ndipo apa lonjezo lirilonse limene Mulungu anapanga mu Baibulo, limodzi lirilonse la ilo, liri mmenemo mwabwino basi monga ilo linali nthawizonse. Ndi oralo! Nchiyani chimapangitsa mpingo kukhala wotere? Ife tiri mu m’badwo wa Laodikaya, pamene iye akuyenera kubwera mwanjira iyi. Ora lake ndi lino la zimenezo.

<sup>99</sup> Koma kumbukirani, mmenemo muli ora limene namwali wogona anabwera kuti adzagule Mafuta, ndipo ora lake linali lomwelo limene Mkwati anadza. Ife tikupeza lero, a Episcopalian, Presbateria, ndi zipembedzo zosiyanasiyana, amene, zaka pang’ono zapitazo, inu simukanawachita ganyu kuti abwere pozungulira gulu la okhulupirira Achipentekoste. Ndithudi ayi. Koma ndi awo pamenepo, lero, akubwera. Kodi inu simukudziwa zimene Yesu ananena? Iwo anabwera kudzagula Mafuta, ndipo anati, “Tipatseniko ena a Mafuta anu.” Iwo amene anali ndi Mafuta, anati, “Sichoncho ayi. Pitani mukagule Iwo, kuwopa . . . kwa iwo amene amagulitsa Iwo.” Ndipo pamene iwo ankayesera kuti agule Iwo, pamene iwo ankayesetsa kuti awapeze Iwo! Kodi inu mukudziwa ora limene ife tikukhalamo, anthu Achipentekoste? Pamene iwo anadzabwera, iwo mwina anali ndi chisokonezo, iwo mwina anachita *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*; koma, molingana ndi Malemba, iwo sanawapeze Iwo. Pamene iwo anali kuyesetsa kuti achite izo, iwo mwina anadutsa mu zotengeka zonse, ndipo kenako mu timalingaliro tonse ndi zogirigisha, koma mdierekezi akhoza kutsanzira zinthu zonsezo. Pamene iwo anagula Iwo, kapena kuyesetsa kuti awapeze Iwo, Mkwati anabwera, ndipo iwo amene anali ndi Mafuta analowa mkati.

<sup>100</sup> Ndipo ndi limenelo ora limene ife tikukhalamo. Ife sitinayambe taliwonapo ilo. Yesu ananena kuti zikanadzatero, ndiye izo ziri chomwecho! Kodi ife tikuwona chiyani? Ife tikuwona Mawu, amene Mulungu anati adzachitika mu tsiku lino, akuchitika pansu pa nkhope zathu pomwe. “Oh, ndiye galamukani, inu oyera mtima a Ambuye, mukugoneranji pamene chimaliziro chayandikira; tiyeni tikonzekere kuyitana komaliza kumeneko,” pakuti sitikudziwa kuti kudzachitika liti. Inde.

<sup>101</sup> Kachitidwe kathu ka mdziko, kachitidwe kathu ka mpingo,

kachitidwe kathu ka chipembedzo, kachitidwe kathu konse, kayipitsidwa ndipo kavunda. Zomwe tikusowa lero ndi zomwe anali nazo dzulo. Uko nkulondola. Zikuwoneka ngati kuuma, kwa mipingo, nkovuta kuwupezanso mpingo umene uli wamoyo ndi Mawu ndi Mzimu wa Mulungu, ndi zinthu zazikulu zikuchitika monga zinkakhalira osati kale kwambiri.

<sup>102</sup> Tsopano, ife tikupeza kuti Mulungu akudziwa chimene iwo ankasowa, chotero Iye—Iye nthawizonse amayankha lonjezo. Ndi Mawu opambana awa omwe ife tikuwawona, lonjezo, iwo an kayenera kudziwa kuti izo zinali ndendende basi zomwe Mulungu analonjeza, zomwe zikanati zidzachitike mu tsiku limenelo.

Inu mukuti, “Motani, chinkayenera kudzachitika chinali chiyani?”

<sup>103</sup> Yesaya 9:6, mneneri anati, “Kwa ife Mwana wabadwa, Mwana wamwamuna, Mwana; Mwana wamwamuna wabadwa, Mwana waperekedwa: ndipo Dzina Lake adzatchedwa ‘Wauphungu, Kalonga wa Mtendere, Mulungu Wamphamvu, Atate Wosatha’; ndipo ulamuliro udzakhala pa mapewa Ake, ndipo Ufumu Wake sudzatha.”

<sup>104</sup> Ife tikudziwa kuti ife tinkayenera kudzakhala ndi Mwana akubadwa mu tsiku limenelo, namwali an kayenera kudzayima ndi kudzabala Mwana. Ndipo Iye sanabwere kudzera mu kachitidwe kawo kalikonse, chotero iwo sanafune kanthu kochita ndi Iye. Iwo anamukana Iye. Koma Mawu odzozedwa, Mulungu (Emanuele) atapangidwa thupi pakati pawo, anayima pamenepo, Iye anati, “Ndani wa inu angakhoze kunditsutsa Ine za tchimo, kusakhulupirira? Fufuzani Malemba, pakuti mwa iwo inu mumaganiza kuti muli nawo Moyo Wamuyaya, ndipo iwo ndi amene akuchitira umboni za Ine.” Iye anazindikiritsidwa bwino kuti Iye anali Mesiya, Mesiya woti adzatenge malo mu tsiku limenelo. Ndipo kachitidweko kanali—kanali katasokoneza malingaliro a anthu, mu malamulo ambiri a dongosolo, ndi zina zotero, mpaka iwo anapangitsa Mawu a Mulungu kukhala opanda mphamvu. Iwo sanathe kuwona kuti Iye anali Mesiya.

<sup>105</sup> Ndipo monga izo zinachitira izo nthawi imeneyo, chomwechonso izo zachita izo kachiwiri. Kulondola. Kachitidwe ka dziko, zimango, zaika mapistoni pamene—pamene paipi yotulutsa utsi ikuyenera kukhalapo, mu zimango zawo zazikulu. Ndipo chotero iyo ingayende bwanji? Iyo siyingachite zimenezzo. Siinamangidwe mwanjira imeneyo.

<sup>106</sup> Mpingo sungayende popanda Mphamvu ya Mulungu, kudzera mu Mawu. Ndipo Mzimu Woyera udzatsimikizira kochha Mawu a Mulungu, pakuti ndicho chimene iwo ukuyenera kuchita. Kudzoza ndi kwakuti kudzawatsimikizira Mawu.

<sup>107</sup> Ndipo Yesu anali Wodzozedwa Ameneyo, Mawu atasandulika thupi. Ndi chifukwa chake Iye anayenda kupita

mmadzi uko, Iye anali Mawu akubwera kwa mneneri. Iye anabatizidwa ndi mneneri. Ndipo mneneriyo kenako anawuka, ndipo anati, “Ine ndikuyenera ndichepe; Iye akula.” Ife tikupeza kuti iyo ndi njira ya Mulungu yochitira izo.

<sup>108</sup> Koma kodi iwo analandira Iwo? Iwo ankeyenera kuwaziwa Iwo. Iwo ankeyenera kuwona machitidwe a Mulungu. Iwo anawawona Mawu akukwaniritsidwa. Iwo ankadziwa Malemba ananena zimenezo, koma iwo sanathe kukhulupirira kuti Iwo akanadzabwera monga choncho. Iwo ankeyenera kubwera mwina kwa Afarisi kapena Asaduki. Ngati iwo akanabwera kwa Afarisi, Asaduki sakanawalandira Iwo. Chimodzimidzi mbali inayo, a—Asaduki sakanawalandira Iwo, chifukwa iwo anati Afarisi adzakhala ndi Iwo.

<sup>109</sup> Ndipo umu ndi momwe izo zikukhalira lero, kachitidwe kathu, ndipo chinthu chonsecho chinavunda ndi kuyipitsidwa. Oh, mai! Ora limene ife tikukhalamo tsopano, dziko lochititsidwa khungu, tikuyenda mu mdima, oweramitsidwa mu kachitidwe ka dziko lino, monga nkhusa zopanda m’busa. Pamene iwo anali ndi Mawu a Mulungu wamoyo atatsimikiziridwa pamaso pawo, ndipo nkuchokapo pamenepo mwakhungu, ndipo anawasiya Iwo, inu mungayembekezere bwanjichi china chirichonse? Amen. Ndi ife pamenepo.

<sup>110</sup> Ndiye, dziko likugawanika pakati. Chifukwa chiyani? Mawu omwewo amene anamangiriza ilo pamodzi akanidwa. Ife tikuzipeza zimenezo mu Ahebri, mutu wa 11.

<sup>111</sup> Einstein anatero. Ine ndinali kumvetsera ku zophunzitsa za iye, kuno usiku wina, New York City, kumene anapanga imodzi ya zophunzitsa zake zomaliza. Iye anali kuyankhula za kuwundana, nyenyezi zazing’ono, izo zinali, uko mu kuwundana. Iye anati, “Ngati munthu atayamba kudutsa mu mlengalenga, kumayenda pa liwiro la kuwala . . .” Nchiyani chimenecho, eyiti sauzande. . . [Wina akuti, “Handirede ndi eyite-sikisi sauzande.”—Mkonzi]. Mailosi handirede ndi eyite-sikisi sauzande pa mphindi. “Izo zingamutengere iye handirede, kumutengera iye zaka za kuwala handirede ndi fifite milioni kuti akafike kumeneko.” Iye anapeza Muyaya. Kenako anati, “Kuti adzabwerere, zingamutengere iye zaka handirede ndi fifite milioni zina, zomwe zingakhale zaka firii handirede milioni. Ndipo dangalo, limene iye angati wapita kuchokera pa dziko lapansi, lingangokhala zaka fifite zokha.” Ndi zimenezotu, kutulukira mu Muyaya! Oh, mai! Ukulu wa Mulungu, pamene Iye anapanga dongosolo lonse la zammwamba!

<sup>112</sup> Ndipo mkasidi uyu, tsiku lina, akuwuluka cha ku Russia uko, ndipo anati iye “sanawone Mulungu, Angelo.” Momwe anthu angakhalire osadziwa! Pamene. . .

<sup>113</sup> Mulungu! Ndipo dongosolo lonse la dzuwa, Iye analiwuzira ilo kuchokera mmanja Mwake; ndipo Iye akukhala zaka

mamillioni ochuluka kwambiri, zaka za kuwala, kupitirira zimenezo. Ndipo chinthu chonsecho chagwiridwa ndi Mphamvu Yake ndi Mawu Ake. Aleluya! Nyenyezi iliyonse ikuyenera kupachikika pamalo ake. Inde, bwana! Ndiye, anali wodzichepetsa mokwanira kutsika pansi ndi kudzapangidwa mmodzi wa ife, kuti adzatifere ife; ndife opanda chowiringula. Ngati imodzi mwa nyenyezi zimenezo ingasunthe kuchoka m'mphako zake, kuchoka mu njira yake kumene iyo ili, ngati izo zingasunthe, zingakhudze dongosolo lonselo. Kachitidwe konseko kakuyenera kutembenuka chimodzimodzi basi, chifukwa chimodzi chimadalira chimzake.

<sup>114</sup> Ndipo kachitidwe ka Mulungu, pamene iko kali mu chiyanjano changwiro ndi Iye, chinthu chonsecho chimagwira ntchito mwangwiro. Ndiko kulondola, chifukwa chikuyenera kutero.

<sup>115</sup> Koma mpingo sunatenge kachitidwe ka Mulungu, iwo unapanga kachitidwe kake kake. Ndicho chifukwa chake tonse tiri kunjira kwa mgwirizano. Ndi chifukwa chake mpingo wasokonezeka kwambiri. Ndi chifukwa chake dziko likugawanika pakati lero, chifukwa tatenga kachitidwe kathu kathu. Ndi chifukwa chake dziko la ndale ndi logawanikana. Ndi chifukwa chake dziko lachipembedzo lagawanika pakati, ndi chifukwa chakuti ife tatenga kachitidwe mmalo motenga dongosolo Lamuyaya la Mulungu la mibadwo. Amen. Ndi limene liri vuto ndi dziko. Ndizo ndendende zimene zavuta, ndi chifukwa chakuti iwo atenga chinachake. Izo zawapangitsa anthu kumati, “Ndine wa Presbateria. Ndine wa Methodisti. Ndine wa Umodzi. Ndine wa Patatu. Ndine . . .” Oh, chifundo! Nzosadabwitsa kuti sitingathe kugwirizana pamodzi, palibepo chirichonse chimene chingatigwirizanitse ife pamodzi.

<sup>116</sup> Bambo Nixon ananena ndemanga yomveka bwino imene ndaimvapo purezidenti aliyense kapena wachiwiri kwa purezidenti akunena mu zaka pang'ono zomalizirazi, pamene ananena tsiku lina, “Vuto ndi chiyani ndi anthu aku America, ataya chikondi ndi ulemu kwa wina ndi mzake.” Monga nzika zaku America zikuwomberana wina ndi mzake, mu msewu, ife tingatani? Mai!

<sup>117</sup> Ngati simungatsemphane ndi munthu, ndipo nkumukonda iye nthawi yomweyo, ndiye mukhale chete. Ngati simungathe kumuza iye, monga bambo akumukonza mwana wake, ndi nkono wololera kuwuyika iwo pakhosi pake ndi kumukumbatira iye pambuyo pake, kulibwino muzisiye izo zokha. Inu simunapite patali mokwanira, inueni, kudziwa chimene inu mukuchikamba. Kulondola. Ine ndikhoza kutsemphana ndi munthu, ndithudi; komabe iye ndi m'bale wanga, ine ndidzagwira dzanja lake. Ine sindingamulole iye kuti azipitirira ndi zimenezo; ngati ine nditero, ngati ine sindinamuwuze iye, ine sindingakhale m'bale wolondola kwa iye. Uko nkulondola.

Koma ine ndikhoza kumuuzwa iye, ndipo kumuuzwa iye kuti ine ndimamukonda iye, ndi kutsimikizira izo kwa iye, ine ndimamukonda iye.

<sup>118</sup> Inu simukuyenera kumuwombera iye, pa msewu. Ine ndimatsutsana ndi Bambo Kennedy ndi—ndi ndale zake, ndi chipembedzo chake, ndi zina zotero, koma iye samayenera zimenezo. Ayi, bwana. Ayi, ndithudi. Palibe munthu amayenera zimenezo.

<sup>119</sup> Chotero, ife tikupeza kuti dziko lonse lavunda. Fuko lathu, ndale, kachitidwe kachipembedzo, ndi chirichonse, izo zavunda.

<sup>120</sup> Izo zikungodikirira. Mawu a Mulungu, amene analoseredwa kwa tsiku lino, akuyembekezera winawake kuti abwere ndi kudzawatsimikizira Iwo. Ndikudabwa ngati Iye wachita kale izo? Ndiye ife tiri kuti ndiye ngati Iye anachita izo? Ngati Iye anachita izo, ndiye ife tiri kuti? Zomvetsa chisoni kwambiri!

<sup>121</sup> Ine ndanenapo chinthu cholimba chokhudza Akazi a Kennedy, nthawi zingapo, cha iwo kukhazikitsa mafashoni a mdziko, ndi mamedwe a tsitsi a phanke awa, ndi, “Momwe alongo athu ndi iwo amametera tsitsi lawo, ndi kuvula monga Akazi a Kennedy,” ine ndinati, “monga Yezebeli wakale.” Izo nzoona. Ine ndikukhulupirira zimenezo. Ine—ine—ine ndikuwamvera chisoni amayi aang’onowo kumeneko usikuuno, ndi ana ake, chimodzimodzi.

<sup>122</sup> Koma ndiroleni ine ndikufunseni inu chinachake. Ngati Jacqueline Kennedy akanamva Mauthenga omwe ena a inu Achipentekoste mwawamva, okhudza kudula tsitsi lanu ndi zinthu, iye mwina sakanadula nkomwe tsitsi. Inu mukuyenera kukhala achipentekoste, ndipo inu mukuchitabe zimenezo! Uh-huh. Uh-huh. Iye mwina sakanakhoza kuchita zimenezo ngati iye akanakhala nawo mwayi ndi kuwumva Uthengawo, mwaona, umene inu mwaumva. Ndi zimenezotu pamenepo. Ife tiri pamalo oyipa, abwenzi. Ndizo kulondola ndendende. Inde, ndithudi. O Mulungu, momwe makhalidwe, chinthucho. . .

<sup>123</sup> Ukazi ndi chimodzi mwa zinthu zomwe zimagwirizanitsa dziko lathu pamodzi. Ndi nsana. Ndipo ukazi, ukoma wabwino umene Mulungu anapereka kuti mkazi akhale mayi, bwanji, iwo—iwo—unapita. Kale litali a—a—a—akazi a mdziko lino, ukoma wa iwo, unagonjera ku mulungu wamkazi wa kachitidwe ka Hollywood; kumadzipanga okha, ndi kudziveka okha, ndi kumachita monga ena a akatswiri a Hollywood awa amachitira. Ndipo nthawi zambiri zimakhala kuti ngakhale kuvula kopanda umulungu, kudolola kofuna kugonana, kumatengedwa ngati mafashoni mmipingo. Ndipo azibusa kuseri kwa guwa, opanda a—opanda kulimba mtima, opanda—mphamvu ya Mzimu Woyera; monga Loti atakhala pansu pamenepo, akuvutitsa moyo wake, ndipo mochuluka kwambiri chiphaso cha chakudya kuti awauze anthu kuti izo nzolakwika. Eya.



<sup>124</sup> Chomwe tikusowa lero ndi kuzizulapo. Tikhoza kuzizulapo mochedwa kwambiri tsopano. Ora likhoza kukhala kuti linadutsa. Ife sitidzakhalanso ndi chitsitsimutso china. Ine ndikudziwa inu mukuyembekezera icho, koma ine sindikuchiwona icho mu Lemba.

<sup>125</sup> Ine ndikuyembekezera Mkwatulo, wa anthu ongodzadza mdzanja. Ndiko kulondola, anthu ongodzadza mdzanja. Iwo sadzasowedwa konse mdziko. Pamene iwo adzapite, inu simudzadziwa konse kuti apita. Ndiko kulondola. Iwo udzabwera ngati mbala usiku.

<sup>126</sup> Ndipo ngati Iye safupikitsa ntchitoyo, chifukwa cha Osankhidwa! Pali ena osankhidwira ku Moyo Wamuyaya, ife tikudziwa zimenezo; onse a iwo, amene ali ndi Moyo Wamuyaya. Ndipo ngati iwo—ndipo ngati iwo... kapena ndiye Iye safupikitsa iyo, chifukwa cha iwo, palibe mnofu umene uti udzapolumutsidwe. Dziko lakumana ndi chiwonongeko chake, zaka thuu sauzande zirizonse. Ife tikudziwa kuti kachitidweko kagawanika pakati. Iko kanagawanika pakati mmasiku a Nowa. Masiku a Khristu, iko kanagawanika pakati. Ndipo apa ndi 1964 akubwera, kodi iye akusiya chiyani? Zaka sarte-sikisi ku zina thuu sauzande; twente-wani, twente-wani za mmahandiredi zikubwerazi. Chimachitika ndi chiyani? Ntchitoyo ikuyenerabe kuti ifupikitsidwe. Yesu anati, a—chivundi cha tsiku lino, “Osankhidwa akanadzanyengedwa ndipo sakanadzapolumutsidwa, ngati kukanakhala kotheke.” Ndi ife apo. Ndipo kalendala imatiuza ife, molingana ndi sayansi, kuti ife tiri pafupifupi zaka fifitini kuchokera pamene. Ife tiri mmbuyo pa kalendala ya Chiroma, molingana ndi kalendala ya Chiyuda, kuti ife tatsalira ndi zaka fifitini, twente pa izo.

<sup>127</sup> Chotero ndiye ife tiri pati? Ife tikuwona mafuko akusweka, ndipo Israeli akuwuka, zizindikiro zimene Baibulo ili linaneneratu za tsiku lino. Ife tikuwona zinthu za zimango zikuchitika. Tsopano Mzimu, mphamvu za Mawu olonjezedwawo, kuti ilowe mu Mpingo Wake ndi kuwapititsa iwo ku Kalvare kutaliko, ndi ku Mkwatulo! Ndipo ndi ife pamene.

<sup>128</sup> Nzosadabwitsa kuti tikugawanika pakati, palibepo kalikonse... Chinthu chomwecho chimene chinalenga dziko lapansi, Chinthu chomwecho chinayikidwa pano kuti dziko lapansi lizizungulirapo, Chinthu chomwecho chimene kachitidwe ndi china chirichonse chinali choti chizizungulirapo, Mawu awa amene, mwa Mulungu, anawumba dziko lapansi. Einstein ananena mu zakezo, anati, “Pali kufotokoza kumodzi kokha kwa Lemba... Kufotokoza kumodzi kokha kwa momwe dziko lino linadzapezekera,” anati, “zimenezo ndi Ahebreri 11, ‘Mwa chikhulupiriro timamva Mawu a... ndi Mawu a Mulungu, kuti mayiko anapangidwa pamodzi ndi

Mawu a Mulungu.” Ndizo zonse. Palibe mmodzi amene angadziwe momwe ilo limazendewera umu mu mlengalenga, ndi momwe lingatembenekire ndi kupanga maora ake twente-foro kuzungulira equator, zina zotero monga choncho, ndi kuzungulira kanjira kake, konsekonse, ndi kubwereranso pa malo omwewo ndipo osaphonya konse mphindi. Ndipo nyenyezi iliyonse ikutembenuka mu mkombero wake monga choncho, ndi kumathandizana ina ndi imzake pamene izo zikupita mozungulira.

<sup>129</sup> Momwe mwezi umenewo umayang'anira pansipo pa nyanja imeneyo! Ngati mwezi umenewo utangosuntha pamalo ake, ife tingaphimbidwe ndi mapazi handiredede a madzi, mu mphindi chabe, kapena awiri. Mwezi umenewo! Penyani, ngakhale inu mukhoza kuboola dzenje apa, anthu inu amene mukubowola mafuta, kubowola pansu apa. Mukuona momwe gombe latalikirana ndi inu? Inu mudzabowole dzenje pansu apa mu nthaka, ndipo mudzawone mu nthawi ya usiku, momwe mafunde amabwerera, iwo adzabweretsa madzi chokwera mu paipi yanu, madzi anu a mchere. Ndithudi. Ndi chiyani chimenecho? Mwezi umenewo umalamulira izo, kumeneko.

<sup>130</sup> Ndi kachitidwe ka Mulungu. Ndi dongosolo la Mulungu. Ilo ndi Lamulo la Mulungu. Koma, ife timapanga lathu lathu, ife sitimatenga Lake. Tiyeni tifulumire tsopano, kuti timalizitse. Monga nthawi imeneyo, ndi chimodzimidzi Khrisimasi iyi, tikulipeza dziko lathu likugawanika pakati. Oh!

<sup>131</sup> Mulungu anadzozedwa, ndipo Iye analonjeza Mawu Ake. Iye anatidzoza ife kumbuyo uko, ndipo Iye anatiuza ife, anawauza iwo, “Pamene Iye anamudzoza Yesu Khristu. . .” Petro ananena pa Tsiku la Pentekoste, iye anati, “Yesu Khristu, Munthu wotsimikiziridwa ndi Mulungu pakati panu ndi zizindikiro ndi zodabwitsa, zimene Iye anachita pakati panu; inu eni mukudziwa.” Iwo ndi mboni. Komanso anati, “Pambuyo pa chiwukitsiro, ndi zina zotero, momwe Iye anachitira! Momwe ndi manja oyipa inu munamutenga Kalonga wa Moyo ndipo munamupachika, Amene Mulungu anamuukitsa; ndipo ife ndi mboni.” Momwe Nikodemo anadzabwera ndikuti, “Rabbi, ife tikudziwa. Ife Afarisi, Mabwalo a milandu a Sanhedrin kumtunda uko, ife tikudziwa kuti Ndinu Mphunzitsi wotumidwa kuchokera kwa Mulungu. Palibe munthu angachite zinthu zimene Inu mukuchitazi pokhapokha izo zitakhala za Mulungu.” Iwo ankadziwa kuti lonjezo limenelo linali la kumeneko, ndipo iwo ankadziwa kuti ilo linalipo, koma kachitidwe kawo kanali katawamangirira iwo kwambiri mpaka samatha kuchita kalikonse za izo.

<sup>132</sup> Chomwechonso izo ziri lero, chinthu chomwecho. Inu simungathe kuchita izo, mudzasiya khadi lanu lachiyanjano nthawi yoyamba yomwe mudzachite zimenezo. Inu mudzangochitira ndemanga uko pa Mawu a Mulungu amenewo

nthawiyina, mudzawone zimene zimachitika; inu mwathedwa. Simudzakhalanso wotchuka. Inu mudzathamangitsidwa pakati pawo, ndi china chirichonse.

<sup>133</sup> Oh, ngati muli ndi utumiki wawung’ono, iwo adzakugwirani inu chifukwa cha ndalama zomwe angamapeze, kukokera gulu pa utumiki wanuwo, kukokera ndalama ndi zinthu. Koma mungoyang’ana pamene izo zidzafika ku Mawu, mudzawawone iwo momwe amachokera pa Iwo. Kodi mukuganiza kuti mtumiki wa Mulungu samadziwa zimenezo? Chabwino, Yesu ankadziwa ngakhale kuti Yudasi anali pakati pa Iye. Nchifukwa chiyani Yesu sananene kanthu kwa Yudasi? Chifukwa chomwecho chimene izo ziri lero, inu mukuyenera kudikirira mpaka ora limenelo lidzafike la chinyengo chimenecho. Uko nkulondola. Iwo anapeza izo. Iwo adzazipeza izo.

<sup>134</sup> Zindikirani, koma iwo sanafune njira yomwe Iye anabwerera, momwemonso izo ziri lero. Mipingo nthawi imeneyo inkafuna kuti kachitidwe kawo kadzozedwe. Afarisi ankafuna kuti kachitidwe ka Afarisi kadzozedwe, Asaduki ankafuna kachitidwe ka Asaduki, Aherodia nawonso, ena otero. Ndi momwemo lero. Ngati iwo atero. . . Ngati Mulungu adzatimize kudzoza, ndi kuwadzoza a Oneness, oh, mai, kodi iwo sadzawauza a Twoness za izo, kapena a Threeness, kapena chirichonse chimene icho chiri? Kodi a Assemblies sadzawauza a Oneness za izo? “Ndinakuuzani kuti ife timalondola!” Amethodisti angawauze Abaptisti, “O mnyamata, mwaona, ife tiri naye iye!” Inu mukufuna kuti kachitidwe kanu kadzozedwe.

<sup>135</sup> Koma Mulungu anangolonjeza kuti adzadzoza Mawu Ake. Amen! Ine ndikudziwa kuti izo ndi zotentha, koma icho ndi chimene chiri Choonadi. Mulungu samasintha konse. Iye amawadzoza Mawu Ake. Inde, bwana. Odzozedwa, Mawu olonjezedwa a m’badwo umenewo ndi omwe Mulungu amawadzoza. Mawu olonjezedwa a m’badwo umenewo!

<sup>136</sup> Lero iwo akufuna kachitidwe ka maphunziro, (chifukwa chiyani?) kuti azikhoza kuchita chirichonse chimene iwo akufuna, ndipo nkumagwiritsitsabe ku zodzinenera zawo za Chikhristu. Oh, ngati iwo ali ndi chinachake chachikulu kwambiri, kumene inu mukhoza kukalowamo, kupita pansu pa mizere, ndi zinthu, ndi kumatafuna chingamu, ndi—ndi kumamenyana wina ndi mzake m’mbali; ndi kupita kunja ndi kukakhala ndi mabwalo achisangalalo ndi zinthu, kumene inu nonse mumapita kukasewera basketball ndi zinthu monga zimenezo. Ine ndiribe kalikonse kotsutsa basketball, baseball, mpira, kapena chirichonse chomwe icho chiri, chachikulu. . . ngati ndizo zonse zomwe mulungu wanu ali, ndi chikwama chachikulu cha mpweya. Koma ndiloleni ndikuuzeni inu, chimene tikusowa lero ndi Mawu a Mulungu, odzozedwera m’badwo uno, zimenezo zidzabweretsanso Mphamvu ya Mzimu Woyera kachiwiri. Inde, izo ziri bwino, koma zimenezo si za mu

tchalitchi. Ayi, bwana. Mukuyenera kumanga chinachake chonga chimenecho, kuti mpingo ukhale pamodzi, inu kulibwino muziwotche izo kapena kuzikankhira izo panja, kapena kutengeramo chinachake mmenemo chimene chiti chidzawabweretsenso Mawu kachiwiri. Ndipo zimenezo ndi zinthu za mdziko, oh, kuzisakaniza izo ndi Mawu a Mulungu, inu simungakhoze kuchita zimenezo. Ayi, bwana.

<sup>137</sup> Inde, bwana, tsopano iwo akufuna kachitidwe. Dziko likutenga kachitidwe. Tsopano ife tikupeza, kachitidwe kakang'ono kalikonse mwa iko kokha, kalikonse ka izo kamati, “Ine ndikufuna Iwo abwere kwa ine. Ine ndikufuna Iwo abwere kwa wanga.” Oh, iwo akupeza makina aakulu, ndi kuwaphunzitsa alaliki, ndi zinthu monga zimenezo, ndi kuwatulutsako iwo, kuwaswa iwo, mnyamata, ndi luntha; mpaka, mai, munthu amamverera mawu ake, galamala yake, ndi yoyipa kwambiri, iye amadana ndi ngakhale kuti apite pa guwa kuseri kwa ilo. Koma zomwe tikusowa lero si kachitidwe ka maphunziro, si mndandanda wa zowerenga.

<sup>138</sup> Chimene tikusowa lero ndi Uthenga wogwiridwa ndi Mphamvu ya Mulungu, kukatsimikizira Mawu a ora lino, kumene kudzabwere winawake yemwe adzaimirire ndi kutchula chakuda “chakuda,” ndi choyera “choyera,” winawake amene angayime ndi kunena Choonadi, kaya Icho chisupula chikopa kapena kukukwiyitsani inu, kapena chimene Icho chingachite. Ndizo ndendende chimene—chimene ora likufuna, lero.

<sup>139</sup> Koma anthu akufuna chinachake. Anthu lero, akazi, akufuna chiyani? Iwo akufuna a—a—anthu, m’busa, amene angayime ndi kuti, “Ziri bwino. Inu mukhoza kuchita *ichi*, kapena kuchita *icho*. Kapena, izo ziri bwino, palibe cholakwika ndi *zimenezo*, wokondedwa.” Mlaliki ameneyo akusowa chikwapu cha Uthenga; kulola tsitsi lodula, kudziphoda.

Ayi, inu mukuti, “Kodi izo ziri ndi chochita chiyani ndi Iwo?”

<sup>140</sup> Kodi simukudziwa kuti kunja kwanu kumawonetsera zomwe ziri mkati? Kodi Baibulo silinena kuti simukuyenera kuchita zimenezo? “Si zodziwika kuti mkazi azipemphera chomwecho.”

<sup>141</sup> Ndipo iwe mwamuna umafuna chinachake chonga choncho? Alaliki, inu simungathe kunena zimenezo, chifukwa inu musiya khadi lanu la chiyanjano, bungwe lalikulu lidzakuthamangitsani inu ngati munganene chinachake cha izo. Mulungu amuthandize munthu yemwe angaganize mochuluka za khadi la khonsolo kapena khadi la chiyanjano kuposa momwe angachitire ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, ndi Mawu! Ungathe bwanjji Mzimu Woyera, umene unalemba Baibulo, kukana zomwe Iye analemba?

<sup>142</sup> “Chabwino, masiku a zozizwitsa, oh, ife sitikuzisowa zimenezo lero. Machiritso Auzimu, zinthu zina izi, kuti, palibe

chinthu choterocho. Zimenezo ndi zam’bwebwe, ndizo, oh, kuwerenga maganizo.” Iwe, wosauka, wonyozeka, chavuta ndi chiyani ndi iwe? Ife tikusowa—tikusowa Uthenga, ngati Mzimu Woyera uli mwa inu!

<sup>143</sup> Ngati ine nditakuuzani inu, “Moyo wa Beethoven unali mwa ine,” ine ndikanatha kulemba nyimbo. Ngati Beethoven akanamakhala mwa ine, ine ndikanamakhala moyo wa Beethoven. Ngati Shakespeare akanamakhala mwa ine, ndikanamapeka ndakatulo. Ine ndikanamalemba masewero, ngati Shakespeare akanamakhala mwa ine.

<sup>144</sup> Ndipo ngati Yesu Khristu akukhala mwa inu, ntchito zomwe Iye ankachita, ndi Mawu Ake, Iye ndi Mawu, zidzadzitsimikizira Zokha tsiku lino, mwa lonjezo lomwelo limene Iye anapereka. Ameni. Ndicho chimene Mulungu akuyembekezera. Icho chimene chimaligwira dziko, moligawaniza, chimene chimaligwira dziko pamodzi, dziko lachipembedzo pamodzi, ndi Mawu Ake, chimagwira aliwonse a Mawu pamodzi. Eya.

<sup>145</sup> Anthu amafuna kachitidwe ka mtundu umenewo, mulimonse. Iwo akapeza kameneko. Iwo ali kale mmenemo, pakali pano. A World Council of Churches adzawapatsa iwo basi chimene iwo akuchifuna, aliyense wa iwo pamodzi. Momwe Achipentekoste awa angakhaliye mmisonkhano iyi, ndi kukalowa mu Mzinda wa Vatican ndi kukalemba kalata yopita kulikonseko, ndi kuti, “Chinthu chauzimu kwambiri chimene ine ndinayamba ndanenapo, pamene ine ndinakhala pafupi ndi Atate Woyera Papa *Wakuti-ndi-wakuti*,” ndi kukhala wa Chipentekoste ndi kudziwa momwe. . . Ndi kuyenda kwakufa kwa Chipentekoste. Chinthu chonsecho ndi chakufa. Icho chavunda. Icho chapita! Icho chabwerera mu Chitaganya cha Mipingo kumene icho chiri. Kulondola ndendende.

<sup>146</sup> Koma Mpingo wa Mulungu wamoyo, Mkwatibwi ameneyo, ukusunthira chitsogolo chimodzimodzi basi. Ndipo Iwo udzapita mu Mkwatulo, mwa Mawu, uko nkulondola, Mawu ndipo Mawu adzabwera pamodzi. Ngati ife tiri gawo la Khristu, gawo la Iwo, ife tikuyenera kukhala Mawu Ake, chifukwa Iye ndi Mawu. Kulondola. Inde, bwana.

<sup>147</sup> Iwo akana Mawu odzozedwa a lonjezo, a m’badwo uno, ndipo Iye nthawizonse ndi Mawu. Ngati Mulungu anatumizira ife odzozedwa, Mawu olonjezedwa panonso, a m’badwo uno, mu 1946, Iye adzakhala yemweyo amene Iye anali pamene Iye anabwera pachiyambi, Mawu odzozedwa a m’badwo. Ahebri 13:8 akuziponyeranso izo pa chilolo chanu, ndikuti, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Ndiko kulondola ndendende. Ndipo ife. . . Ndipo Iye adzakhala ndi Mawu olonjezedwa a Atate a m’badwo uno. Ngati Yesu abwera, Iye adzakhala ndendende basi chimene Mawu anati Iwo akanadzakhala mu m’badwo uno.

<sup>148</sup> Ndicho chimene Eliya anali mu m'badwo wake. Ndicho chimene Mose anali mu m'badwo wake. Ndicho chimene Nowa anali mu m'badwo wake. Ndicho chimene, kulikonseko, mneneri aliyense ankabwerapo. Ndipo a—Mawu, pamene Iwo anadza mu chidzalo, Mawu onse anapangidwa thupi pakati pathu, Iwo anachita ndendende basi zomwe Iwo anati Iwo akanadzachita mu m'badwo umenewo.

<sup>149</sup> Ngati Iwo angabwere lero, Iye angakhale ndendende basi Yesu Khristu kukhala moyo lonjezo Lake la zomwe Iye analonjeza kuti adzachita, basi monga Mawu.

<sup>150</sup> Iye anali Mawu. Yesaya 9:6 ndi Yesu Khristu. Ndipo pamene Iwo anasandulika thupi ndi kudzakhala pakati pathu, Iwo anakhala moyo ndendende basi chimene Iwo anachita. Mose ananena kumeneko, mu Bukhu la Eksodo, “Ambuye Mulungu wanu,” kapena Deuteronome, “Ambuye Mulungu wanu adzazutsa mneneri, wofanana ndi ine; ndipo kudzachitika, kuti yense amene sadzamumvera Iye adzadulidwa pakati pa—anthu.” Ndipo pamene Iye anabwera, Iye anachita chimodzimidzi basi chimene Mawu anati Iye akanadzachita. Ndipo anamupezero Iye zolakwika, chifukwa kachitidwe kawo kanali katawadula Iwo ndipo anapanga Mawu a Mulungu kukhala opanda mphamvu kwa iwo. Mukuona? Iwo amalephera kukhulupirira zinthu zotero monga Izo. Iwo sakanakhulupirira zinthu za mtundu umenewo, chifukwa izo zinali zitadutsa nthawi, mwakuganiza kwawo. Oh!

<sup>151</sup> Pakuti, Iye watsimikizira Mawu Ake kuti ndi omwewo. Iye akanadzatsimikizira Mawu lero, monga Iye anawatsimikizira Iwo nthawi imeneyo. Iye angadzatsutse, mwaukali, kachitidwe kachipembedzo kalikonse mu dziko, ngati Iye angabwere pa dziko lapansi lero. Ndicho chimene Iye anachita, poyambirira. Ndicho chinthu chimene Iye akanati adzachimenye. Ndicho ndendende chimene Iye anachimenya pamene Iye anabwera poyamba. Monga Iye anachitira nthawi imeneyo, chomwecho iwo akanati adzachite nthawi ino, aponso. Ndipo Iye anatero nthawi imeneyo, pakuti Iye samasintha Mawu Ake. Iye samasintha kachitidwe Kake. Izo nthawizonse zimakhala chimodzimidzi, Ndi Mawu odzozedwa nthawi iliyonse, a m'badwo. Uko nkulondola.

<sup>152</sup> Chomwechonso kachiwiri, monga ife tikuzipezero izo lero, ngati Iye abwera, Zolinga zake zogwirizanitsa dziko lapansi pamodzi zidzakanidwa chimodzimidzi monga momwe zinakhallira nthawi imeneyo.

<sup>153</sup> Koma mvetserani, potseka, ine ndikufuna ndinene ichi. Ife sitinalonjezedwe kachitidwe, ife sitinalonjezedwe chipembedzo, chipembedzo chapamwamba, dongosolo lapamwamba la mtundu wina. Koma ife tinalonjezedwa Ufumu, Ufumu Wamuyaya. Amen. Ndicho chimene ife tinalonjezedwa, kukhala

ndi Moyo Wamuyaya mu Ufumu Wamuyaya uwu. Ndipo Boma likulamuliridwa ndi Mfumu Yamuyaya, Mawu Ake Amuyaya operekedwa kwa anthu Ake omwe ali ndi Moyo Wamuyaya. Ndipo anthu a Moyo Wamuyaya samadya pa zinthu za mdziko, koma kunalembedwa, kuti, “Munthu adzakhala moyo ndi Mawu aliwonse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.” Chotero pamene ife tonse tsopano. . . Ife tilandira Ufumu uwu, ndipo ife timapeza kuti, “Zonse ziwiri kumwamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu awa sadzapita konse.” Ndipo Mawu awa ndi Ufumu. Iyi ndi Mfumu ndi Ufumu, Kachitidwe, Moyo, chinthu chirichonse chiri *Apa*.

<sup>154</sup> Ngati Mulungu amaweruza dziko Lake pogwiritsa ntchito mpingo, mpingo wake utiwo umene Iye ati adzaliweruzire ilo? Ilipo ingati pamenepo? Mahandirede ndi mahandirede ndi mahandirede a mipingo ya zipembedzo zosiyanasiyana. Ngati wa Katolika uli wolondola, ndi Katolika wake utiyo? Ngati ndi wa Chigriki Katolika uli wolondola, ndiye kuti wa Chiroma ndi wolakwa. Ngati wa Chiroma uli wolondola, wa Chigriki ndi wolakwa. Chotero, inu mwaona, ngati wa Methodisti ukulondola, wa Baptisti ndi wolakwa. Ngati wa Baptisti uli wolondola, wa—wa Pentekoste ndi wolakwa. Ngati wa Pentekoste ukulondola, ndiye wa Presbateria ndi wolakwa. Mukuona? Koteru inu nonse mukhoza kusokonezeka kwambiri.

<sup>155</sup> Koma Mulungu sanatisiye ife opanda mboni iliyonse kapena uliwonse—uliwonse—muyezo uliwonse umene ife tikuyenera kuyimapo. Amenewo ndi Mawu awa! Iye anati, “Mulole mawu a munthu aliynse akhale bodza, ndipo Anga akhale Choonadi.” Uko nkulondola.

<sup>156</sup> Pakuti, “Zonse ziwiri miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka.” Ife tikuuzidwa apa, kuti, “Tidzalandira Ufumu umene sudzatha kusunthidwa.” Inde, bwana. Pamene maufumu onse achidziko awa akugwa tsopano, ndipo dziko lonse likugawanika pakati, komabe ife tikubatizidwira mu Ufumu umene sungathe kusunthidwa. Ameni. Ife tikulandira Ufumu. Chotero, pamene dziko likugawanika pakati, ife tikubadwira mu Ufumu uwu umene sungathe kugawanika pakati. Ndi Mawu Amuyaya a Mulungu, ndipo ife timayima pa zimenezo. Iwo sangathe kugawanika pakati.

<sup>157</sup> Ife timamva zambiri za zimene kachitidwe katsopano aka kadzabweretse, kachitidwe kachipembedzo, inu mukudziwa, kadzabweretsa mtendere pa dziko lapansi, pamene Akatolika ndi Achiprotestanti onse adzalumikizane pamodzi. Ena a iwo amakhulupirira mu machiritso Auzimu, ena samakhulupirira, ndipo ena amakhulupirira *ichi*, ndipo ena amakhulupirira *icho*. Ndipo inu mukuyenera kusiya mkangano wanu wawukulu womwe mwakhala mukukangana nthawi zonse, chikhulupiriro chanu cha uvangeli, kuti mulowe mu World Council. Ndipo chipembedzo chirichonse chiyenera kuti chidzalowe

mnenemo. Chotero, ngati chipembedzo chiri chotembereredwa, ndipo kukhala wa icho, kodi izo zidzachita chiyani? Izo zidzakuponyerani inu mmbuyo momwe. Ngati Roma ali mayi wa chipembedzo, ndipo iye ndi chirombo ndi chilemba cha chirombo, ndiye iwo anapanga fano kwa icho, bungwe, mipingo yonse pamodzi ikupanga fano kwa chirombo, molunjika kumene kubwerera ku chilemba cha chirombo kachiwiri! Kachitidwe ka mdziko, zachipembedzo, zabweretsa kachitidwe kobweretsa chilemba cha chirombo.

<sup>158</sup> Ndipo inu mukuziwona izo monga momwe ine ndikuziwonera, kuti pakali pano izo zikakamizidwa, kuti, onse omwe sali mnenemo zomwe zayikidwa kale mu dongosolo, makina aakulu akhala pamenepowo; zimango ziri pamenepo zikuyembekezera Satana kuti alowe mu izo, ndi zimphamvu. Mukuona? Ndipo, pamene izo zidzatero, palibe munthu adzathe kulalikirira Uthenga, sipadzakhala munthu, amene sali mu kachitidwe aka. Ndi chimenecho chilemba cha chirombo. Ndipo kumbukirani, pa nthawi imeneyo, Mkwatibwi adzakhala atapita, chotero inu mukuwona momwe izo zayandikirira. Chabwino, chotero inu mukuwona pamene ife tiri.

<sup>159</sup> Mukhoza kuwona chimene: kutsika kwakukulu uku, zinthu izi zomwe iwo akupitirira nazo. “Oh, galamukani, inu oyera a Ambuye, mukugoneranji pamene chimaliziro chiri pafupi?” Chifukwa chiyani inu mukuchita zimenezo? Nthawiyina inu mudzachimwira tsiku lanu la chisomo. Inu musadzachite konse zimenezo. Inde, bwana.

<sup>160</sup> Tsopano, dongosolo ili silidzabweretsa mtendere wa mdziko. Ngati zimenezo zidzabweretse mtendere wa mdziko, chinachitika ndi chiyani kwa Kalonga wa Mtendere amene anali Mawu? Ndi wotsutsakhristu mu chiphunzitsa chake. Ndi zotsutsana ndendende ndi zimene Mulungu ankaziyimira, zomwe Iye anatiuza ife. “Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akukhulupirira,” iwo amakhulupirira kuti zimenezo ndi zamkutu. Machitidwe 2:38 ndi chinthu china, kwa iwo, iwo sakudziwa kanthu za izo. Mawu onse, ndi zina zotero, iwo sadziwa kanthu za Iwo, ndipo iwo amawakana Iwo. Zimakwaniritsa ndendende zomwe mneneri ananena mu Timoteo Wachiwiri, mutu wa 3, “Iwo akanadzakhala ammutu, odzikweza, okhala nawo mawonekedwe aumulungu, ndipo akanadzakana Mphamvu yake, mmasiku otsiriza.”

<sup>161</sup> Kachitidwe ka chipembedzo kameneko ndi chilemba cha chirombo. Inu mwadziwa. Ngati simunandimvepo ine ndikunena izo, ndi chifukwa chake ndavutikana nazo izo zolimba. Chifukwa tsopano ine ndikuganiza kuti nthawi yatsala pang’ono kutha, chotero mwina ndikhoza kuzilola kuti izo zibwere ndi kunena Choonadi cha izo. Ndi uyo apo. Ndicho chilemba cha chirombo, ndendende. Roma anali chirombocho, ndipo iye anali chipembedzo, bungwe loyambirira.



<sup>162</sup> Ndipo ife tinatuluka mwa iye, ife anthu Achipentekoste, kuti tisakhale otenga nawo gawo a izo; ndi kupotokera mmbuyo momwe, “monga galu ku masanzi ake, ndi nkhumba ku matope ake,” kubwerera mkatimo. Nzosadabwitsa dongosolo lathu la Chipentekoste latha, ndipo chomwechonso a Methodist, Baptist, World Council of Churches, ndi onse! Iwo akumezedwa mu World Council of Churches, kupanga chizindikiro kapena—kapena fano kwa chirombo, kuti achipatse mphamvu yake. “Ndipo icho chinali ndi mutu wovulazidwa mpaka ku imfa, ndipo kenako kukhala ndi moyo,” Roma wachikunja kupita ku Roma wa upapa. Oh, mai, momwe Achiprotestanti akhalira akhungu! Ndipo ndi inu pano, pakali pano mwakhala pakati pomwe pa zimenezo. Ndipo palibe chimene mungachite tsopano. Kachitidweko kanapangidwa kale. Iwo adzachitenga icho ndipo osadziwa kuti achitenga icho. Iwo adzangokhala mmenemo, ndizo zonse. Iwo sangatulukemo mmenemo. Izo zachitika kale.

<sup>163</sup> Izo si zachilendo kwa anthu, apobe. Izo zalalikidwapo. Kumbukirani, Mulungu anapereka umboni wa izo, anatsimikizira izo ndi Mawu Ake. Zinthu zimene Iye anati Iye akanadzachita, Iye anachita izo ndendende basi. Chotero, ndi zopanda kuwiringula. Inde.

<sup>164</sup> Ndi zimango zabadza. Zabweretsa zinthu ndendende zomwe Yesu anachita, “Inu ndi miyambo yanu mwapangitsa Mawu a Mulungu kukhala opanda mphamvu.” Chifukwa chokana Mawu owona amenewo, iwo abwereranso mu chinthu chomwecho kachiwiri, ziphunzitso zawo ndi chinthu chomwecho monga iwo anali pachiyambi, ndi, zimenezo motsutsa Khristu, kuphunzitsa Mawu kwa okhulupirira mu m’badwo uno ndi kuwauza iwo kuti—kuti awakane ndi kuzikana.

<sup>165</sup> Pamene Mulungu anawapanga Mawu Ake thupi pakati pa anthu Ake, mu m’badwo wa Yesu Khristu, pa Khirisimasi yoyamba, kunachita chiyani kusuntha kwa Afarisi ndi zipembedzo zonsezo? Anati, “Musadzapite konse ku umodzi wa misonkhano imeneyo. Ngati inu mudzatero, mudzachotsedwa pamene mudzachite zimenezo.”

<sup>166</sup> Kodi inu simukuwona momwe zinthu zinabwerezedweranso? “Kodi Munthu uyu ndi ndani? Kodi Iye anachokera ku sukulu iti? Kodi Iye ali ndi khadi la chiyanjano chiti? Kodi Iye ali ndi gulu liti? Kodi Munthu uyu akuchokera kuti?” Monga, Iye akubwera lero monga Iye anachitira nthawi imeneyo. “Ife sitidzakhala naye Munthu uyu kuti azitilamulira ife. Ife sitidzakhala ndi aliyense woti azitiuza ife zoti tichite. Ndife a Oneness. Ndife a Threeness. Ndife a Presbateria. Ndife a *ichi*. Ife sitikuyenera kuti tizikhala ndi Iwo!”

<sup>167</sup> Ine ndikudziwa inu simutero, koma inu mwina mutenga Mawu kapena muwonongeka! Ndizo zonse. Ndizo palibe njira yina koma Iwo, koma Iwo ndi omwe amatigwirizanitsa ife

pamodzi. Ufumu wa Mulungu si ufumu wa izi, si choncho, Ufumu wa Mulungu si kachitidwe ka dziko lino. Yesu ananena chomwecho. Yesu anati, “Ufumu Wanga si wa dziko lino. Ngati ukanakhala woterewo, nthumwi Zanga zikanamenyera.” Iye ndi Mawu.

<sup>168</sup> Ife tiri ngati Abrahamu. Abrahamu analandira Mawu. Ndipo chirichonse chinali chotsutsana ndi Mawu, iye ankachitcha icho ngati kuti icho panalibepo. Ndipo mwana woona aliyense wobadwa wa Mulungu amalandira Mawu a Mulungu, ndipo, ine sindikusamala zomwe aliyense anena, chimene kachitidwe kakuyankhula motsutsa Mawu amenewo, Mawu ndi owona, mulimonse.

<sup>169</sup> Mulungu amakhala wokakamizika kukumana nanu pamaziko a malonjezo amenewo. Kunja kwa malonjezo amenewo, Iye sangakumane nanu inu, chifukwa inu mwadzichotsapo nokha kwa Iye. Ndi chifukwa chake dziko lathu likugawanika pakati. Potseka, tikhoza kunena izi.

<sup>170</sup> Chirichonse chimene chiri chotsutsana ndi Iwo, chiri ngati kuti icho palibepo. Kachitidwe kopangidwa ndi munthu koteroko, ife sitimayang’ana konse pa zimenezo. Ayi, bwana. Kubatizidwira ndiye mu Ufumu uwu, ife tsopano tikukhala mmalo Ammwambamwamba mwa Khristu Yesu, oh, mai, ndi Mfumu yathu yodzozedwa limodzi nafe; kudyerera pa Ufumu Wake, Mawu olonjezedwa odzozedwa ndi otsimikiziridwa pakati pathu pomwe. Amenii. Psyii! Ndi zimenezotu, lonjezo Lake la Ufumu litapangidwa patsogolo pathu pomwe, palibe chimene chingakuchotseni inu kwa Iwo. Ayi, bwana.

<sup>171</sup> Abrahamu, ngakhale kuti mkazi wake anali wokalamba, ndipo iye akukalamba nthawi zonse, sizinamuvutitse iye mpang’ono pomwe. Iye sanadzandime konse pa lonjezo la Mulungu, kudzera mu kusakhulupirira. Ziribe kanthu mutanena mochuluka bwanji kuti, “Ndi zosatheka. Iye sangakhoze kuchita nazo izo,” iye anakhala ndi Iwo, mulimonse. Chifukwa chiyani? Mfumuyo inali naye iye, kumuwonetsa iye masomphenya ndi kumuwonetsa iye zimene zikanadzachitika, ndipo zinachitika monga momwe Iye ananenera, ndipo iye anadziwa kuti ameneyo anali Mulungu.

<sup>172</sup> Ndipo pamene Mulungu apanga lonjezo ndipo inu nkuliwona ilo, ndipo Iye nkulinena ilo ndipo ilo nkumachitika, ndi kumanena ilo ndipo ilo nkumachitika, ndi kumanena, ilo nkumachitika, ndipo osamalephera konse, ndi Mulungu wa tsikulo. Oh, kudyerera pa malonjezo Ammwambamwamba awa a Mawu Ake olonjezedwa a m’badwo uno, oh, podziwa, ndi chitsimikizo chamtheradi cha chikhulupiriro, kuti pakubwera miyamba yatsopano ndi dziko lapansi latsopano. Amenii. “Kumwamba kwatsopano ndi dziko lapansi latsopano, pakuti kumwamba koyamba uku ndi dziko lapansi loyamba

zidzachoka.” Koma kumwamba kwatsopano uku ndi dziko lapansi latsopano, Paulo ananena pomwe apa mu Bukhu la Ahebri, wa twente- . . . 14:25, iye anati, “Pakuti ife talandira Ufumu umene sungasunthike.” Kodi ife tinalowa chotani mmenemo? Osati mwa kachitidwe kachipembedzo; koma, Ufumu wa Mulungu uli mkati mwanu. Ufumu! Mfumu ndi Mawu Ake ndi ofanana, ndipo Iwo ali mkati mwanu, akutsimikizira ora limene ife tikukhalamo tsopano. Lonjezo limene Mulungu analipanga kwa m’badwo uno, ife tiri pano, tikukhala ndi Mfumu, titakhala mu malo Ammwambamwamba, tikumuwona Iye akuchita zinthu izi.

<sup>173</sup> Ndipo ife tingachokeko bwanji ku Mawu amenewo, nkupita ku kachitidwe kena? Kodi izo zimachita chiyani? Iwo amakana Mawu. Inu mukuyenera kulandira kuti mukane Choonadi, inu musanakhale ndi cholakwika. Uko nkulondola ndendende. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi].

<sup>174</sup> Ora limene ife tikukhalamo, O Mulungu, dziko likugawanika pakati! Apo zapachikika pazopachikira, mabomba, apo papachikidwa chinthu choti chichite ndendende basi.

<sup>175</sup> Mpingo wakonzeka. Iwo wasindikizidwira mkati, wakonzeka kuti uzibwera. Padzakhala kutsanulira kwakukulu kwa Mzimu, inde, bwana, kuti kudzawugwire Mpingo umenewo ndi kudzawutengera Iwo mu mlengalenga. Ndendende. Chifukwa, mwaona, Mpingo, Mawu, Mkwatibwi. . . Ndipo, Khristu, utumiki Wake uli mwa Mkwatibwi Wake, amene ali Thupi Lake, Thupi lakumwamba, kapena ine ndikutanthauza kuti, a—Thupi Lauzimu la Ake kuno pa thupi lauzimu pa dziko lapansi, Mzimu Wake uli mmenemo ukukhala Moyo Wake kunjwa komwe, mpaka Iye ndi Mpingo adzakhala amodzi mu chikwati. Mwaona, iwo adzakhala mmodzi. Iye adzawatenga iwo, owerengeka chabe mmasiku otsiriza.

<sup>176</sup> Ndipo kenako anamwali onsewo amene anagona, kutsika kudutsa mu m’badwo, iwo onse anawuka, inu mwaona. Tsopano, zimenezo zidzakhala pa ulonda wachisanu ndi chiwiri, m’badwo wa mpingo wachisanu ndi chiwiri, wotsiriza, nthawi yotsiriza, Laodikaya, pa mapeto, pamene gulu lapang’ono chabe la iwo linalowamo. Koma, zimabweretsa chiukitsiro chonse cha onse amene anafa m’mibadwo yawo, kukhala moyo ku Mawu amenewo amene anadzozedwa ndi Mulungu ndipo analalikidwa kuti adzachitike mu tsiku limenelo, pamene ife timadutsa mu mibadwo ya mpingo imeneyo ndipo tinawona ndendende Mawu amene akanadzakomana nawo iwo mu nthawi imeneyo; momwe Luther anadzukira, momwe ife tinapezera, mu m’badwo wa Luther, chinapita chirombo chonga nkhope ya munthu pa icho, ndipo anapita, amene anali “wokonzanso,” kutanthauza *munthu*. Ndipo, pamene, mibadwo yonse, uliwonse unakwaniritsa ndendende basi zofunikira za Mawu a Mulungu.

<sup>177</sup> Ndipo chomwechonso m'badwo uno udzakwaniritsa ndendende ku chizindikiro ndi chodabwitsa ndi chinthu chimene Mulungu analonjeza kuti adzachita mmasiku otsiriza ano. Ndipo Mpingo Pawokha udzakhala wokonzeka ndipo udzapita mu Mkwatulo ndi Yesu, chifukwa, "Tidzalandira Ufumu umene sudzatha kugwedezeka. Iwo sungathe kusunthidwa. Miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Ufumu uwu sudzachoka konse." Ameni. Ndine wokondwa kukhala, usikuuno, ameni, usikuuno, mu Ufumu umenewo. Kodi sindinu okondwa kukhala mwa Iwo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Oh, mai, kukhala mu Ufumu, Umenewo!

<sup>178</sup> Tangoganizani, kodi inu mungadzilonjeze nokha chiyani lero? Mu zaka zina teni mpaka fifitini, ngati dziko lidzakhalepo, ngati ilo lingapirire izo, mwamuna aliyense mu Shreveport, mkazi aliyense, mudzayenera kudzanyamula mfuti, pa msewu, ndi inu, mthumba mwanu, kuti mudziteteze nokha. Zigawenga! Inu mudzaziletsa bwanji izo? Yeserani izo. Chabwino, chonsecho...

<sup>179</sup> Ine ndinali mu New York, sabata lina. Ndipo ndinapita kudutsa kumeneko, kwa mailosi, kunalibe kalikonse koma zigawenga izi za usinkhu wa zaka za mmatini zokhala ndi ndolo m'makutu mwawo, ndi tsitsi losapesa, atavala zothina, ndi atsikana okhala ndi ma bikini aang'ono, iwo ankazitcha izo, kumapitirira monga choncho, kunja pa msewu. Ndipo anthu amayenera kuwapatsa iwo ufulu wa njira. Oh, vuto ndi chiyani ndi dziko lino? Ndi chifukwa chakuti—chizindikiro cha kuvunda kwa makhalidwe oyipa, fuko lokanidwa ndi Mulungu. Ndizo zonse.

<sup>180</sup> Inu mungamange bwanji pa zowotchedwa za mabwinja ena ngati amenewo? Inu mudzachita bwanji zimenezo, pamene zigawenga zikuyenda mu msewu ndi kuwombera Parezidenti amene mu galimoto yake yomwe?

<sup>181</sup> Ndipo usiku wina, bambo wa nyumba ya pamsewu, akupanga phokoso ndi chirichonse, anangolowa mmenemo ndipo analumphira pamaso pa apolisi a Texas ndi oposa handiredi ndi chinachake atayima pamenepo, anayenda kulowa mkati; ndipo aliyense akumuyang'ana iye, anasolola mfuti yake ndi kuwombera munthu mopanda chisoni, ndi kuchokapo. Iye adzanena kuti ndi "wamisala," ndipo adzamasulidwa.

<sup>182</sup> Mu mzinda wathu womwe, mwamuna analowa mu garaja, tsiku lina, atavala chipewa, ndipo anamutenga a—a—mwamuna amene anali—wogulitsa magalimoto. Iye sanamukonde iye, ndipo iye anangotulutsa mfuti ndi kumuwombera iye, kanayi kapena kasanu. Ndipo iye anati iye anali wamisala; iwo anamusiya iye. Ngati ndi "misala" yochonderera munthu ameneyo, ndiye kuti Oswald nayenso anali ndi mwayi, akanatha kukhala ndi mwayi wochonderera misala.

183 Ndi chiyani chimenecho, mulimonse? Inu mukuona pamene izo ziri, chinthu chonsecho ndi mulu waukulu wa chivundi! Chinthu chonsecho ndi cholakwa, ndipo dziko lonse likuyima lolakwa, ndipo mpingo ukuyima wolakwa pamaso pa Mulungu. Amen. Nzosadabwitsa kuti tikugawanika pakati!

Tiyeni tipemphere.

184 Ambuye Mulungu, ife tiri pano. Ora lafika, Atate. Zikhoza kukhala kuti nthawi yatha kuposa momwe tikuganizira. Mwinamwake chivundi chalowamo, ndipo chimbalinga chakhala chikudya, ndi chirimamine, mpaka Moyo wonse wapita. Ine ndikukupemphani Inu, Ambuye, kuti mutichitire chifundo. Perekani, Ambuye, ngati pali mwamuna kapena mkazi, mnyamata kapena mtsikana, mu Kukhalapo tsopano, yemwe sakukudziwani Inu, kuti iwo akulandireni Inu pakali pano, Atate. Ilo likhoza kukhala dzina lotsiriza limene liti lipite pa Bukhu, kuchokera ku Shreveport.

185 Ndipo pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa. Kodi munthu ameneyo ali pano mungakweze dzanja lanu, munene kuti, “M’bale Branham, ine ndakhutitsidwa kwathunthu kuti zomwe inu mwanena ndi zoon. Dziko likugawanika pakati, ndipo ife tikulandira Ufumu umene sungathe kugawanika pakati. Ndipo, kwa ine, ine sindikutsimikiza ngati ine ndiri mu Ufumu umenewo, kapena ayi.”

186 Musadalire kuti munakhalapo ndi mtundu wina wa zomverera zodzipangitsa. Inu musadalire pa zakuti inu munayankhulapo mmalirime. Ine ndimakhulupirira mu zinthu zimenezo. Ndithudi, ine ndimakhulupirira mu kuyankhula mmalirime. Koma ine ndamvapo adierekezi akuyankhula mmalirime ndi kupereka kutanthauzira kwake, kulemba mu malirime osadziwika, afiti, mwaona. Inu simungayendere zimenezo.

187 Koma ngati Moyo wa Yesu Khristu uli mwa inu, Iwo udzazikhala moyo Wokha, kukhulupirira Mawu aliwonse a Mulungu. Chifukwa, Iye sangazikane Yekha, Iye ndi Mawu.

188 Tsopano, ngati Iye ali Mawu, ndipo Iye ali mwa inu, ndiyeno inu mukuti, “Chabwino, M’bale Branham, ine ndikukuuzani inu, ine sindingakhoze basi kuwatenga Iwo. Ine sindikuwakhulupirira Iwo, zinthu izi ndi za tsiku lino,” ndipo apa Iwo alonjezedwa ku tsiku ili, oh, m’bale wanga, iwe wanyengedwa. Mzimu wina wafika pa iwe ndipo wakunyenga iwe.

189 Dona, ngati iwe, kapena mwamuna, kapena aliyense amene iwe uli, ngati zinthu izo zomwe ziri zenizeni kwambiri, zenizeni mu Mawu, zimene Yesu Khristu anafera; osati kungokhala ndi mpingo kapena kukhala ndi gulu lotengeka, koma kukhala ndi gulu lomwe liri ndi Mzimu Wake, ukukhala mwa Iye; Mkwatibwi Wake, Mawu Ake ali mmenemo, Mawu aliwonse ndi owona.

Ndipo inu mukudziwa Iwo samagwira ntchito kupyolera mwa inu mwanjira imeneyo, inu mukudziwa kuti muli zinthu, mu Baibulo, zimene inu simungakhulupirire kuti ziri choncho; ndipo inu mukufuna kuti mukumbukiridwe mu pemphero? Tsopano ndi diso lirilonse litatsekedwa, mutu uliwonse utaweramitsidwa, ine ndikudabwa, ngati pa ora lakumapeto ili pamene. . .

<sup>190</sup> Izo zikhoza kukhala pafupifupi kudutsa nthawi yomverera, mwaona, chifukwa idzafika nthawi yonga imeneyo pamene Mzimu wa Mulungu udzachotsedwa padziko lapansi, sipadzakhalanso. Mpingo udzakhalabe kwa kanthawi, uko nkulondola, ukulalikira, chifukwa iwo ukuyenera kulalikira kwa otayika Mwamuyaya, basi monga momwe utumiki uliwonse unachitira, kubwera mmusi kudutsa m'badwo. Gawo lotsiriza la utumiki uliwonse kulalikidwa kwa otayika Mwamuyaya. Ndipo padzakhala utumiki tsopano umene uti udzalaliki kwa otayika Mwamuyaya iwo atakana kulandira Iwo.

<sup>191</sup> Koma ngati pakuwoneka kuti pali moto mu mtima mwanu, kuti mukufuna kukhala ndi Khristu mwa inu, ndipo dziko lonse lafa, kodi mungakweze dzanja lanu, ndikuti, “Ndikumbukireni ine mu pemphero, M'bale Branham.” Ambuye akudalitirani inu. Inde, inde, manja teni kapena fifitini. Kodi pangakhale wina tisanapemphere? Tsopano tikukonzekera kuti titseke, mu pafupifupi maminiti awiri kapena atatu. Mulungu akudalitse iwe, dona wamng'ono.

<sup>192</sup> Tangoganizani za zimenezo, taganizani, taganizani za izo, bwanji ngati nthawi yatha kwambiri? Nanga bwanji ngati inu muli munthu womaliza amene Iye angagogode pakhomo?

<sup>193</sup> Ilo likugawanika pakati, ife tikudziwa zimenezo. Inu simungakhale pano, ndicho chinthu chimodzi chotsimikizika. Simungakhale pano. Inu mukupita. Mungolembe izo, inu mukupita. Ndipo ngati inu muli. . .

<sup>194</sup> Basi sikuti mungogirigishidwa. Musanene kuti, “Ndine wa tchalitchi.” Inu mukhale otsimikiza za Zimenezo. Ngati Khristu sakukukhalani moyo, mwa inu, mpaka inu muta. . . malingaliro anu onse, mtima, solo, thupi.

<sup>195</sup> Inu, inu mukuti, “Chabwino, ine ndikuganiza. . .” Inu mulibe lingaliro likubwera, m'bale. Mulole malingaliro amene anali mwa Khristu akhale mwa inu! “Ine ndikuganiza kuti masiku sakuyenera kukhala. . .Ndikuganiza kuti *izi* sizikuyenera kukhalapo. Ine ndikuganiza Mawu sakutanthauza *izi*.” Ife tiribe lingaliro limene likubwera.

<sup>196</sup> Ngati malingaliro a Khristu akhala mwa ife, ndiye ife tidzawazindikira Mawu amenewo kukhala Choonadi, ndipo Iwo azikhala moyo mwa ife. Inu simungachitire mwina, Iwo ndi Khristu!

<sup>197</sup> Mudzachotse moyo kuchokera mu mpesa wa mavwembe ndi kudzawuyika iwo mu mpesa wa dzungu, iwo udzabala

mavwembe. Inu simungathe kuwuletsa iwo ku izo, chifukwa moyo umene uli mmenemo uli.

<sup>198</sup> Ndipo ngati—ndipo ngati mukuti, “Chabwino, ine sindimakhulupirira Iwo, a—Mawu apa,” ndiye umenewo si Mzimu wa Khristu. Mwaona, muli mzimu wina mwa inu.

<sup>199</sup> Kodi pali wina tisanapemphere? Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, ndi inu, inu. Inde, izo nzabwino. Tsopano, winawakenso, mphindi yokha tsopano. Mulungu akudalitse iwe, mnyamata wamng’ono. Iwe, dona wamng’ono. Iwe, mlongo. Mulungu akudalitseni inu, ndi inu. Chabwino, kodi aliponse wina? Mulungu akudalitseni inu, kumbuyo uko.

<sup>200</sup> Musachite mantha tsopano. Musachite manyazi tsopano. Mawa usiku ukhoza kukhala mochedwa kwambiri. Mukuona? Zikhoza kuchitika usikuuno kuti mtima usiya kugunda. Zikhoza kuchitika usikuuno inu mukukana Iwo, nthawi yanu yotsiriza.

<sup>201</sup> Ndi angati muno alibe ubatizo wa Mzimu Woyera, kwezani mmwamba manja anu, inu mukudziwa kuti—kuti mulibe Iwo? Mai! Umo ndi momwe inu mumaloweramo. Mzimu Woyera ndi Khristu. Umo ndi momwe munasindikizidwira mu Ufumu, Aefeso 4:30, “Musawukhumudwitse Mzimu Woyera wa Mulungu, umene inu munasindikizidwa nawo kufikira tsiku la chiwombolo chanu.” Ndipo ngati inu—ndipo ngati muli ndi lingaliro la Baibulo ili, kuti ilo si lowona, ndiye mzimu mwa inu si Khristu, chifukwa Khristu ndi Mawu.

<sup>202</sup> Apo pali Ufumu umene sungasunthidwe, amenewo ndi Mawu. Umenewo ndi Ufumu umene sungasunthidwe. “Miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Mawu Anga sadzachoka.” Ngati Mawu ali mwa inu! “Ngati inu mukhala mwa Ine, ndipo Mawu Anga mwa inu; pemphani chimene mufuna, chidzachitidwa kwa inu. Ntchito zimene Ine ndikuzichita,” Yohane Woyera 12, 14, “ntchito zimene Ine ndikuzichita inu mudzazichita nanunso; ngakhale zoposa izi, chifukwa Ine ndikupita kwa Atate. Komabe kanthawi pang’ono, ndipo dziko silidzandiwonanso Ine; komabe inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka ku mapeto a dziko lapansi.”

<sup>203</sup> Penyani chimene ntchito Zake zinali, muwone ngati izo zabwerera kwa ife mu masiku otsiriza. Kodi awakana Iwo? Padziko lonse! Ndipo dziko likugawanika pakati, Khristimasi iyi, monga zinachitikira Khristimasi imeneyo.

<sup>204</sup> Atate athu Akumwamba, panali manja ambiri anakwezedwa mmwamba pano usikuuno, mwinamwake sarte kapena forte, mu gulu laling’ono ili la anthu, anakwera mmwamba usikuuno, kuti iwo adziwa kuti iwo sanali kumene iwo akuyenera kukhala. Iwo anadziwa kuti Inu simumakhala mwa iwo, mu Muyeso. Ena, mwinamwake chinachake mu Baibulo, iwo amati,

“Ine basi. . . Ine—ine—ine ndikuvomereza Iwo chifukwa ine—ine ndikungoganza kuti mwina ine ndikuyenera kutero.”

<sup>205</sup> Koma, Ambuye, Inu munalonjeza kuti Inu mudzakhala Mawu, ndipo Inu ndi Mawu. “Ndipo Ine ndidzaza kwa inu, ndi kudzazizindikiritsa Inemwini kwa inu.” Ife tikupeza kuti kachitidwe Kanu, kachitidwe Kanu, sikasintha nkomwe.

<sup>206</sup> Pamene Inu munabwera mu Chipangano Chakale, Inu munati, “Mawu anadza kwa aneneri.” Ndipo pamene Iwo anatero, iwo analosera ndipo Iwo anadzachitika, chifukwa Iwo anali Mulungu.

<sup>207</sup> Tsopano ife tikuzindikira kuti pamene Inu munatitumiza ife, ndipo munatilamulira ife kuti tipite mu dziko lonse ndi kukapanga ophunzira, ndipo Inu munati, “Pamene Iye Mzimu Woyera udzabwera pa inu, Iye adzabweretsa zinthu izi zimene Ine ndakuphunzitsani inu, ku chikumbukiro chanu.” Ndizo, kachiwiri! “Ndipo adzakuwonetsani inu zinthu zirinkudza.” Komabe! “Mulungu, mu nthawi zamakedzana ndi mu njira zosiyanasiyana ankalankhula kwa makolo kudzera mwa aneneri; mmasiku otsiriza ano kudzera mwa Mwana Wake, Khristu Yesu.” Mzimu Woyera Pawokha, ukubwera, Wowulula wa Mawu olembedwa, ndi Wowonetsera wa zinthu zimene zirinkudza! Iwo anati, “Mawu a Mulungu,” mu Ahebri 4, “ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, Ozindikira maganizo amene ali mu mtima.”

<sup>208</sup> Ndipo munthu wochimwa ndi wa mpingo, lero, akhoza kukhala ndi kukuwonani Inu mukuchita chinthu chomwecho, ndi kuwutcha Iwo mzimu *woipa*, chimodzimidzi monga iwo anachitira mmasiku apitawo. “Ngati akumutcha Mbuye wa nyumbayo ‘Belezebule,’” ndipo tikuziwona izo.

<sup>209</sup> Ambuye, Mulungu, tingachitenso chiyani tsopano? Pali mitima yanjala pano yomwe yakweza manja awo. Atengeni iwo pakali pano, Ambuye, dzazani mtima uliwonse ndi chikondi Chanu. Perekani izi.

<sup>210</sup> Ndipo pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa. Ngati inu amene munakweza manja anu mukufuna kubwera mozungulira nsanja pano, musa—musati munyalanyaze izo, mwaona. Mphindi yotsatira yokhayi tsopano, mungonyamuka, mwamsanga kwenikweni, ndipo mubwere pano, mungoyima. Uwu ukhoza kukhala usiku umene inu mulandire Mzimu Woyera.

<sup>211</sup> Abwenzi, taonani, izi sizikhala nthawi zonse. Izi, zidzafika podzatha. Zikutha pakali pano, ndipo mwina zikhoza kukhala kuti zatha kale. Koma bola ngati inu mukuyesera kuti mufikire kwa Khristu, ndiye ndithudi pali chinachake pamene, komabe, chikukukokerani inu njira imeneyo.

<sup>212</sup> Kodi inu simubwera tsopano ndi kudzayima apa ku pemphero? Inu amene mukufuna kutero, mungayende



mozungulira guwa, mphindi yokha, pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa. Tsopano anthu akubwera. Ndiko kulondola, bwerani mudzazungulire guwali. Mudzati, “Dziko likugawanika pakati, sindikufuna dziko mwa ine. Ine ndikufuna Ufumu mwa ine, umene sungagawanike pakati.”

213 Yesu anati, “Palibe chimene chiti chidzatayike. Ine ndidzachiwukitsa icho kachiwiri mmasiku otsiriza. Inde, ndidzachiwukitsa icho.” Iye analonjeza, kuti inu musadzagawanike pakati. Mulungu adzaziwukitsa izo. Ine sindikusamala chomwe icho chiri, Iye adzachiwukitsa icho.

214 Kodi inu mumadziwa kuti palibe chimene chingawonongedwe ndi munthu? Palibe chomwe chingawonongeke. Inu mukuti, “Nanga bwanji moto, pamene ukuwotcha chinachake?” Iwo sumawononga izo. Ndi ma atomu okha mmenemo akuswa zipangizozo, ndipo inu mumatenthedwa nazo izo. Izo zimabwereranso ku chikhalidwe chake chapachiyambi, momwe izo zinali pachiyambi; zidulo, mipweya, magetsi, ndi zina zotero, monga izo zinali. Simungathe kuthetsa psyiti chirichonse. Ngati—ngati dziko litayima motalika mokwanira, ilo likhoza kubwereranso ku chidutswa china cha pepala, kapena mtengo wina, kapena chirichonse chimene inu mukuwotcha. Mwaona, inu simungakhoze kuchithetsa icho psyiti. Mulungu anazipanga izo chomwecho.

215 Oh, simungathe kuchithetsa psyiti chirengedwe cha Mulungu, ndiko kulondola ndendende, chotero ndi mochuluka bwanji momwe Iye angawukitsire icho chimene Iye analonjeza!

216 Kodi inu simubwera? Kodi pangakhale enanso tsopano? Pali gulu laling’ono pano, osafika theka la omwe anakweza manja awo mmwamba. Ine ndimaganiza inu mumatanthawuza izo kwenikweni pamene inu munakweza manja anu, makamaka pa Uthenga wonga umenewo.

217 Ndi angati a inu muno, tsopano ndi mitu yanu yoweramitsidwa, mukudziwa izi, kuti inu mwamuwona Mulungu akusunga lonjezo Lake, pomwe pano kudutsa nsanja iyi, ndipo amadziwa zinsinsi za mu mtima? Imodzi, palibe nthawi imodzi yomwe Iye anayamba wanenapo kalikonse koma zomwe zinachitika. Inu mukudziwa kuti izo ndi zooni. Mmisonkhano, kulikonseko, ndendende basi zomwe Yesu Khristu anachita pamene Iye anali pano pa dziko lapansi, Iye wachichitanso icho. Inu mukudziwa zimenezo. Inu mukuzindikira zimenezo. Ine ndimaganiza za machiritso Ake.

218 Masabata awiri apitawo, ine ndisanapite ku New York, panali dona anabwera ndi khansa pa mmero. Mzimu Woyera unayankhula kwa iye, mu msonkhano. Apa iye anali pamenepo, Lamlungu, ndi khansa mu chidutswa cha sanza, iye anali atayikhosomola iyo. Madokotala anayang’ana pa iyo, ndipo

anati, “Moyo unatuluka mu khansa, ndipo iyo yamasuka.” Ndipo iye anayikhosomola iyo.

<sup>219</sup> Wina anali ndi khansa mu matumbo achikazi. Ndipo iye anali nayo pamenepo, ndi chithunzi chokulitsidwa, ndi zolemba za dokotala pa icho. Iye anali atatulutsa iyo, masiku awiri atadutsa.

<sup>220</sup> Mnyamata wamng’ono atayima pamenepo, yemwe analibe kukumbukira, kuchokera—kuchokera miyezi ndi miyezi ndi miyezi. Iye anagwa ndi kuvulala kuseri kwa mutu wake. Iye sankadziwa ngakhale yemwe iye anali kapena kumene iye anali. Ndi mawu a pemphero chabe, ndi kusanjika manja pa iye, Ine ndinati, “Dzina lako ndi ndani?”

Iye anati, “Billy Dukes.”

Ine ndinati, “Uli ndi zaka zingati?”

Iye anati, “Usinkhu wa zaka naini.” Anati, “Kodi ine ndiri kuti?”

<sup>221</sup> Mphamvu ya Mulungu! Ndikanakonda mukanakhala ndi ine ku Colorado, masabata angapo apitawo, pamene chinachake chinachitika chimene chikanakugwedezani inu, kuti mudziwe chimene icho chinali. Ife tiri ku nthawi ya kumapeto, mzanga.

Osatero, musati muyike izi pambali. Bwerani. Ngati pali wina pano, bwerani kuno. Kodi mutero? Kodi inu mubwera?

<sup>222</sup> Tsopano, ngati inu simukubwera, mwaona, ine—ine sindi, ine—ine—ine—ine. . . Zomwe ine ndingachite ndi kungokuuzani inu Choonadi, mwaona, ndiye izo ziri ndi inu. Monga Nowa, iye analowa, chombo chinatsekedwa kumbuyo kwake, palibe chimene chinachitika kwa kanthawi; koma dziko linawonongeka kunjako, ndipo dziko linapitirirabe kukhala mofanana basi. Mukuona?

<sup>223</sup> Pilato anapitirira, atamupachika Yesu. Ine ndilalikira pa izo, mmausiku angapo, “magazi m’manja mwanu,” Ambuye akalola.

Zindikirani tsopano, kodi alipo wina, ife tisanatseke?

<sup>224</sup> Tsopano ndifunsa akazi ndi amuna odzipatula enieni, amene amudziwa Mulungu, kuti abwere pansu ndi kudzayima apa ndi kudzayika manja pa anthu awa. Iyi ikhoza kukhala nthawi yomaliza imene iwo angakhale ndi mwayi umenewu. Ena a inu anthu odzipatula amene mumamudziwa Mulungu, bwerani ndi kudzayima ndi anthu awa. Iwo ali ndi makadi a pinki pa iwo, pafupifupi aliyense wa iwo, izo zikutanthauza kuti iwo ali, iwo ndi alendo pakati panu. Ine ndikuganiza ndiko kulondola. Bwerani, mudayike manja anu pa iwo. Ena a mamembala a Life Tabernacle, bwerani kuno. Ena a inu abale kuno mukufuna kubwera? Bwerani, ili ndi ora. Kodi inu—kodi inu simukuzikonda izi, anthu? Mai! Kodi changu chathu chiri kuti? Chiri kuti chinachake chathu chimene chimatipangitsa ife kuyendabe? Vuto ndi chiyani?

Tsopano ngati omvetsera angadikire mphindi yokha, ku pemphero ili.

225 Anthu inu amene mwayima pano, tsopano penyani, musadalire pa kutengeka kwina, ngakhale izo ziri ndi kutengeka mwa Iwo. Inu musadalire pa zakuti ngati muti muyankhule ndi malirime, kapena ayi. Musaganize kalikonse za izo. Mulungu asamalira zimenezo, mwaona. Inu mupemphe kuti Yesu Khristu abwere mmoyo wanu ndi kudzakhala moyo Iyemwini mwa inu. Inu simukufuna maganizo ochuluka a inu mwini. Inu mukufuna maganizo Ake. “Mulole maganizo amene anali mwa Khristu akhale mwa inu.” Oh, ichi ndi . . .

226 Izi, chabwino, inu mungomva zinthu izi nthawi yomaliza, kamodzi. Tsopano penyani, ine ndikufuna omvetsera onse kuti ayime pa mapazi anu, kunja uko. Tsopano, inu anthu okonedwa amene mwabwera kuno kudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera, mawa ndi Kuperekamathokozo, palibe kugwira ntchito mawa. Uwu ndi moyo wanu, m'bale, mlongo. Uku ndi kopita kwanu Kwamuyaya. Izi, ndi mwina tsopano kapena ayi. Ndipo bola ngati inu mukumva kukoka kwakung'ono kumodziko! Ndipo tangoganizani za Zoonadi izi, izo ziri patsogolo pathu pomwe. Musakhale akufa pa zinthu zimenezo, anthu. Izo ndi zenizeni. Izo zatsimikiziridwa, zenizeni, zangwiro nthawi zonse. Ndipo ndi Mawu, otsimikiziridwa!

227 Ndikuyang'ana pa mwamuna wayima pomwepa. Sindingathe kuganizira dzina lake. Ine ndikukhulupirira ndi Blair, M'busa Blair. Pamene ine ndinali uko ku Hot Springs, kuno osati kale, ine ndinamutenga kunja uko mwa omvetsera, mwamuna uyo wakhala apo, ndipo mzimu woyipa unkayesera kuti ufike kwa mwamuna ameneyo, kuti umupangitse iye kundikayikira ine. Tsopano penyani chimene chinachitika. Ine ndinati, “Iwe ukhoza kuzandifuna ine nthawiyina, mwaona.” Sizinali koma masabata angapo apitawo mpaka mkazi wake anandiyimbira ine, mwamunayo ankafa. Mukuona?

228 Ndipo munthuyo anavomereza, iye anadziwa ndiye kuti anali mdierekezi akuyesera kuti amupangitse iye kukhulupirira kuti Iwo anali mtundu wina wa chinyengo kapena chinachake. “Koma iye akanadziwa bwanji zimenezo?” iye anaganiza. Chotero ndiye iye . . . Ndi pemphero tinathamangitsa choyipacho mwa iye.

229 Ndipo kenako masabata angapo apitawo, mwaona, Satana anadziwa kuti nthawi imeneyo ikubwera, pamene iye akanakhala atagona pamenepo ndi chotupa ku mbali yake, ine ndikukhulupirira mkazi wake ananena, kapena chinachake, ndi kutentha thupi kwakukulu, chosokoneza mmutu mwake; osadziwa chomwe icho chinali, matenda ena mu mbali yake, anatupitsa mbali yake. Ndipo mkazi wake wamng'ono anandiyitana ine ku Tucson. Ine ndinati,

“Mlongo, inu muli ndi mpango?” Ine ndikukhulupirira iye anali ndi chinachake pamenepo, mpango wawung’ono kapena chinachake. Ine ndinati, “Ine—ine ndikutha kuona iwo. Tengani iwo ndi kuwuyika pa M’bale Blair, mu Dzina la Ambuye Yesu.” Ndipo iye anamupempha iye kuti abwere kudzayimba.

<sup>230</sup> Nanga bwanji ngati Satana akanapambana ndi kumupangitsa iye kusakhulupirira, ndi kudziwa kuti icho chinali pamenepo? Iye sakanakhoza kuyima pano usikuuno ndi Baibulo lake pa mtima wake. Mukuona?

<sup>231</sup> Ndi Satana akuyesera kuti akupangitseni inu kusakhulupirira Izi. Uko nkulondola. Musamvetsere kwa izo. Kumbukirani, “Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Mwaona, zinthu izi zatsimikiziridwa chomwecho.

<sup>232</sup> Tsopano tiyeni tonse, inu pano pa guwa, tiyeni tingokweza manja anu mmwamba, ndi kunena, “Ambuye Yesu, ndithandizeni ine tsopano,” aliyense akupemphera.

<sup>233</sup> Atate athu a Kumwamba, tasonkhana pano, O Mulungu, izo ziri pakati pa imfa ndi moyo, kwa anthu awa ayima pano. Mulole Mzimu Woyera ubwere mmoyo wawo pakali pano. Mulole pabwere Mphamvu ya Mulungu, imene yawabweretsa iwo kuzungulira guwa ili, mulole Iyo ibwere kwa iwo mu chiukitsiro cha Khristu, ndipo ipereke kwa iwo Moyo Wamuyaya wawukulu umenewo umene iwo akuwufuna. Ambuye, mipingo paliponse ikufa, madzi auzimu akuwoneka ngati akuchotsedwa padziko lapansi. Ndipo pamene pali mwayi woti anthu awa abwere pansu pa Kasupeyo, perekani, Ambuye, kuti miyoyo yawo yowuma, usikuuno, yomwe ili ndi njala ndi ludzu la Mulungu, idzazidwe ndi Mzimu Woyera pakali pano. Perekani izi, Ambuye. Mulole chifundo Chanu ndi chisomo zikhale pa iwo.

<sup>234</sup> Tsopano basi—mungoyika mutu wanu... pitirirani kupemphera, musingopemphera. Aliyense, mwaona, musingopemphera. Ine ndikupempherani inu. Ndichita zonse zomwe ine ndingathe, koma sindingathe kukupatsani inu Mzimu Woyera. Mulungu akuyenera kuchita izo. Penyani, mupangeni Khristu patsogolo panu pomwe, mmalingaliro anu. Yang’anani kunjika uko ndi kuwona ngati inu mukumuwona Khristu patsogolo panu, pamene mukutseka maso anu. Kenako muyende molunjika kwa Iye, ndi kunena, “Ambuye Yesu, pano ine ndiri. Inu ndi ine tikhala amodzi kuyambira pano mpakana. Ine nditenga Mawu aliwonse amene Inu mwandiiza ine usikuuno.” Tsopano mungokhala pamenepo, mungopitirira kukhala, ngati mungakhale usikuuno, mawa, tsiku lotsatira, mungokhala mpaka izo zonse zitatha, kupemphera, mukukhulupirira kuti Mulungu akudzazani inu ndi ubatizo wa Mzimu Woyera.

<sup>235</sup> Bwera kuno, Don, atsogolere iwo mu pemphero. Mulungu akudalitse iwe, Don. 

63-1127 Dziko Kamodzinsu Likugawanika Pakati  
Life Tabernacle  
Shreveport, Louisiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)